Msinkhu	size	-fupika	be (too) short
Ukali	fierocity	-opsya	irighthen; be dreadful

Here are various constructions which convey more or less the notions of superiority "more.. than", inferiority "less.. than", equality "as . . as", or plenitude "very much", "too much". Very often these notions are expressed by the context itself, without the need of any additional word. For instance:

**Malo ano achepa** this place is small, or smaller, or too small.

more...than : **Mwana wanga ali wamkulu (: wakula); wanu wachepa.**

My child is bigger than yours. (. . wanu ali wamng'ono).

**Mwana wanga ali wamkulu kopambana wanu (: koposa waru)** adverb

**Kodi ndi inu ndi ine, wamkulu ndani?** Between you and me . . .

**Ndi ichi ndi icho, chabwino ndi chiti?**

**Pa (or Mwa) nyumba ziri panozi, yabwino ndi iti?** Out of these . . .

**Mwana wanga, msinkhu wake, apambana wanuyu.**

**Njinga yanga ili yabwino kopambana yanuyo.**

**Nyumba yake ndi yaikulu; yanga ichepa.**

less...than : **Munda wanga uchepa (: ndi wochepea); ndi waung'ono.**

**Mwana wanga asiyana ndi wanu; nzeru zake ndi zochepea.**

or "not as...as" **Mwana wanga nzeru zake salingana ndi...**

as...as : **Mwana wanga ali wamkulu chimodzimidzi uyu, the same as**

**Mwana wanga msinkhu wake ukunga uyu (: ali wonga uyu)**

**Mwana wanga kukula kwake ali wonga uyu.** his size

**Mwana wang ali wamkulu monga uyu (: ngati uyu).** like, as (adverbs)

**Nyumba yanga kukula kwake ili monga ngati iyo.**

**Mwana wanga msinkhu wake akulingana ndi uyo (: afanana ndi uyo)**

**Ndi mwana wanga ndi mwana wanu msinkhu wao ndi wolingana.**

See the great variety of constructions, and also the inversions, quite common when we have a Possessive; a typical example:

**Kodi mwana wa mphunzitsi dzina lake ndani?**

Very...: **Adamanga nyumba yaikulu kwambiri (: ndithu : zedi)**  
**Ndinadwala kwakukulu (: kwabasi: kopambana extremely)**

**Padzakhala msonkhano waukulukulu** (reduplication of the stem)

**Inali mbalame yaing'onong'ono.**

**Kamwana kakang'onong'ono.**

**Nsaru yakuthaitha worn out.**

**Njinga yakufaiifa completely**

**Nyumba yosesasesa well swept.**

**Malaya abwinobwino.**

too...: **Mwachedwa you are too late.**

**Chingwe chatalika.**

**Wafulumira.**

**Nsungwi yafupika.**

**Ndalama zachepa : zaperewera : ndi zosakwanira.**

**Katundu achuluka ndipo galimoto lichepa.**

How...? **Nyumba yanu ili yaikulu bwanji? (:...ndi yaikulu chotani?)**

**Nyumba yanu ndi yotani kukula kwake? How big is it?**

**Mwana wanu ndi wotani msinkhu wake?**

**Ngongole yako ndi yaikulu bwanji? (: ikwana ndalama zingatii?)**

rather. : **Mwana wake ali wamkulupo. Ana a sukulu achulukapo.**

**Matenda ali bwanji?**

**— Ali bwinopo. (: pang'ono)**

**Anagwira nsomba zingapo. (: pang'ono) Anakhala pano masiku angapo.**

**Anali mmisiri wopanda mnzake. panalibe wina other wolingana naye.**

1. What is the best relish, meat fish or eggs?
2. Here in Malawi the Indians are more numerous than the Europeans.
3. I have many friends; but this is the one whom I like the most.
4. He wears a new hat like mine; but his is white, mine is black.
5. There are many pictures in this book. Tell me, which is the best.
6. I have bought two bundles of bamboos; they are longer than these.
7. Which is the fiercest animal, the lion or the leopard?
8. Rats are bigger than mice, and have a long tail.
9. Which is the first and greatest commandment?
10. My car is not as big as yours, but it carries more luggage.
11. He asked me this question: What is the best, to marry or not to marry?
12. These two shirts are different, but the price is the same. mtengo
13. My younger brother and your sister have the same age. zaka
14. They were born on the same day. But your sister is taller.
15. How long was the snake which you killed yesterday?

**Proverb: Nzimbe sadyera kutalika koma kutsekemera.**

Mbewu	seed, vegetable	-fesa	sow
Mtedza	groundnut	-bzala	plant
Nyemba	bean	-mera	germinate
Mpunga	rice	-berekā	produce, bring forth
Mbatata	potato	-thyola	break off
Duwa	flower Maluwa	-sintha	change
Tsamba	leaf	-kanika	be a failure
Dimba	garden near water	-dzaza	be full

WINA "another, one... the other, some... some, some more". This word takes the Concordial prefix. Note contraction of vowels: the stem is—NA: a-i changes into e: Ena.

- 1 Wina Ena Ndiri nawo agaru awiri, wina wamphongo wina wamkazī.
- 2 Wina Ina Ali nayo minda iwiri wina wantedza, wina wafodya
- 3 China Zina Chingwechi chafupika; mundipatse china.
- 4 Ina Zina Mbatatazi sizikwanira; katengeni zina!
- 5 Lina Ena Tsiku lina tinakomana naye pamsika.
- 6 Wina Ena Ulendo wina tidzapita kunyanja kukagula nsomba.
- D Kena Tina Ngati musowa kanthu kena, mundiuzē! Musaope!  
Moto uja wazima, Katoleni tinkhuni tina!

- 1 Kwina Uyu kuyankha kwake ndi kwina his answer is different.  
Kufesa ndi kwina, kubzala ndi kwina, are 2 different things.  
Pena Ihe timakhala pamudzi pena in another village.  
Njerwa zakupsya zikhale pena ndipo zosapsya pena.  
Pena (: pa malo ena). Pena ndi pena on different spots.  
Iphani mbuzi pena nkumba! (: kapena) either, or.  
Kwina Kafuneni ntchito kwina! somewhere else (: kudziko kwina)  
Kwina kuli chimanga chambiri, kwina kuli njala.  
Alendoŵa achokera kwina ndi kwina from different places.  
Iyeyo kwao ndi kwina, inenso kwathu ndi kwina.  
Mwina Ihe timagona umu, koma iwo amagona mwina (: munyumba ina).  
Palibe nyumba zabwino; mwina muli zoluma, mwina muli makoswe.

Timakomana naye, mwina kumsika, mwina kusitoro sometimes.  
Mphunzitsi sanabwere; mwina wasochera perhaps, possibly.

-berekā produce, give birth (: bala) Mayi wake anaberekā ana asanu.  
carry on the back: Akuberekā mwana kumbuyo.

-kanika : Fodya wakanika. Mvula yakanika. Gule uja wakanika.

WENIWENI "real, genuine, pure". This adjective is always used in the duplicated form; the stem is ENI.

- 1 Weniweni Enieni Mkazi wake weniweni ndi uyu, osati uyo.
- 2 Weniweni Yeniyeni Sakumwa phala koma mowa weniweni.
- 3 Chenicheni Zenizeni Mundiuzē chifukwa chenicheni true reason.
- 4 Yeniyeni Zenizeni Anayamba kumenyana; inalī ndewu yeniyeni.
- 5 Lenileni Enieni Dzina lanu lenileni ndinu yani?
- 6 Weniweni Enieni Ukwati wake suli ukwati weniweni.
- D Kenikeni Teniteni Kankhani kenikeni kamene ndabwera nako ndi aka.
- I Kwenikweni Sindikumva kupweteka kwenikweni koma ndilibē mphamvu.

Penipeni Pakati penipeni pabwalo pali chimtengo chachikulu.  
Ndinapha kalulu; ndinamlasa pamtima penipeni. right

Kwenikweni Kwenikweni mukufuna chiyani? What do you want exactly?  
Kunyanja ndi kutaŵi kwenikweni. really  
Amayi anga alipo; koma sali bwino kwenikweni.

Mwenimweni Tsirani madzi mudzenje mwenimweni!  
Mkati mwenimweni mwa nyumba right in the middle of ...

-kula msinkhu grow up, reach puberty: -tha msinkhu  
-sintha change : -sintha dzina. -sintha ndalama.

1. Have you something else to say? Show me the other picture!
2. One bag is full, the other one is empty. Which is yours?
3. Some bricks are well burned; but others are not.
4. I saw birds of all kinds, some red, others white, others black.
5. My elder brother has two children, one boy and one girl.
6. These two girls have the same mother, but different fathers.
7. What is the name of your real village. Chimutu or Njoka?
8. Are you coming or not? Tell us something definite!
9. We have the same name, but we come from different villages.
10. The boys sleep in one room and the girls in another.
11. Some have planted groundnuts, others beans, others European potatoes.
12. What is the real name of this small animal, in Chicheŵa?
13. If you don't like that red shirt, you can change. Choose another one!
14. I have tried to repair your old bicycle, but it has been a failure.
15. In some places there is much maize, in others there is none.

Proverb: Msonkhamsonkha unang'amba thumba.

Nkhalango	forest, wood	-tema	cut
Nthambi	branch	-cheka	cut, saw
Thabwa	board plank	-pala	plane
Chipatso	fruit	-koma	be good, nice
Nthochi	banana	-ipa	be bad
Malalanje	oranges	-zuna	be sweet; -tsekemera
Mandimu	lemons	-wawasa	be sour, acid
Muzi	root	-wawa	be bitter, ache

**YENSE** This word takes the verbal adjective prefix **wo-**; stem **-NSE**.  
The first meaning is "all, the whole" (notion of totality).  
In connection with the personal pronouns:

- |   |       |              |               |   |
|---|-------|--------------|---------------|---|
| 1 | (ine) | ndense       | I totally     | Ndikudzipereka ndense ku ntchito yanga.     |
| 2 | (iwe) | wense        | (-dzi- p. 76) | I am devoting myself totally to my work.    |
| 3 | (iye) | yense        |               | Ali yense ali wokondwa. Everybody is happy. |
| 1 | (ife) | tonsefe      |               | Tense tipita kumaliro. We all go to the...  |
| 2 | (inu) | nonsenu      |               | Mfumu wakuitanani nonse ku msonkhano.       |
| 3 | (iwo) | onse: onsewo |               | Ndikuwakumbukira onse.                      |

With the different classes of nouns:

- |   |        |       |   |
|---|--------|-------|---|
| 1 | Yense  | Onse  | Anaba katundu yense. Abale anga onse anamwalira.    |
| 2 | Wonse  | Yonse | Mwendo wonse watupa. Werengani midzi yonse!         |
| 3 | Chonse | Zonse | Wadya chipatso chonse. Zipatso zonse zaola          |
| 4 | Yonse  | Zonse | Usadye nsima yonse! Bwezani ndalama zonse!          |
| 5 | Lonse  | Onse  | Ndaona dziko lonse. Lembani maina onse!             |
| 6 | Wonse  | Onse  | Anabvina usiku wonse. Kodi mwaleimba maukwati onse? |
| D | Konse  | Tonse | Kanyumba konse kanapsya. Tolani timiyala tonse!     |
| I | Konse  |       | Mankwala awa amachotsa kupweteka konse.             |

A second meaning is "each, every" or "any"; and then the verb **-li** is often inserted in between the noun and the adjective.

- 1 Mwana aliyense walandira nthochi imodzi. (: Mwana yense...)
- 2 Mnzanga amapita kwao mlungu uliwonse, pa tsiku loweruka.
- 3 Mundipatse chipatso chirichonse! Zonse ndi zabwino.
- 4 Mukufuna ntchito yani? — Iri yonse, palibe kanthu.
- 5 Amabwera kudzacheza nane tsiku lililonse nthawi ya madzulo.
- 6 Usiku uliwonse timamva kulira kwa afisi.
- D Mungathe kuimba kanyimbo kalikonse.
- I Lekani kukwiya kulikonse! Kupweteka kulikonse pali mankwala ake.

**Ponse** Pa muzi paliponse pali mfumu. In every village...  
Ponseponse anthu akudandaula. Everywhere...  
Mungathe kumanga nyumba yanu paliponse. ...on any place.

**Konse** Ndinatuma munthu kumudzi kulikonse. ...to every village  
Anakayenda konsekonse koma sanapeze ntchito. everywhere.  
Mungathe kupita kulikonse, uku kapena uko. anywhere.

**Monse** Munyumba mulimense muli makoswe. In every house...  
M'nyumba mwao umu muli katundu monsemonse. everywhere.  
Mungathe kugona mulimense, umu kapena umo. anywhere.

**Konse** in a negative sentence means "not at all" or "never", according to the context:  
Alibe martha konse. Sindinaone konse njoka yonga iyo.  
Sindivutika konse. Sanapite konse kumudzi kwao.

**Nthawi yonse** always: **Nthawi zonse; Masiku onse.**

-tema	cut across, make incision ... nkhuhi, mitengo, nsungwi.
-cheka	saw, cut slices: ... matabwa, nyama, mbatata, chipatso.
-pala	thabwa plane, -pala moto fetch fire Mwana iwe, kapale moto!
-pala	chibwenzi make friendship: -panga chibwenzi
-wawa	fodya wowawa; mwawa wowawa strong. Mtima undiwawa cause pain.

1. I need some bamboos, but I won't buy the whole bundle.
2. You may come at any time, in the morning, at noon or in the evening.
3. Let everybody bring his own bundle of grass!
4. Don't take all the groundnuts! Leave some in the basket!
5. She showed me all the pictures; they are very nice.
6. In the past there was a wood near each village.
7. Some oranges are sweet, others are sour. You can take them all.
8. You must cut off all the branches which don't produce any fruit.
9. On Sunday everybody wears nice clothes; all are happy.
10. Your daughter is lying; she is not sick at all: She is just lazy.
11. What fruit do you prefer, an orange or a banana? Choose one!
12. Have you counted all the money which is in this bag?
13. Write down the name of every person whom you meet on the way!
14. Do you know the name of this small red fruit?
15. In each basket there are fruit of all kinds. All are for sale.

Proverb: Mawu a akulu akoma akagonera.

<b>Khonde</b>	verandah	<b>-zungulira</b>	go round
<b>Denga</b>	roof	<b>-folera</b>	thatch, cover with grass
<b>Chipinda</b>	room, partition	<b>-mata</b>	plaster wall
<b>Chipupa</b>	wall	<b>-zira</b>	plaster floor
<b>Mpanda</b>	grass fence	<b>-duka</b>	break, be broken
<b>Tsekera</b>	long grass	<b>-mweta</b>	cut grass
<b>Nkhwangwa</b>	axe	<b>-khoma</b>	fix, hammer, pay (tax)
<b>Msomali</b>	nail	<b>-zula</b>	pull off; uproot

**YEKHA** This word means "alone, only", "by oneself". The stem is *-kha*; it also takes the verbal adjective prefix *wo-*.

- 1 **Ndekha** Ndinali ndekha munyumba pamene ngozi inaoneka.
- 2 **Wekha** Anzako onse ali okondwa, koma iwe wekha uli wokwiya.
- 3 **Yekha** Anakumba dzenje yekha panalibe wina womthandiza.
- 1 **Tokha** Ife tokha timakonda nsomba, koma anzathuwa sakudya.
- 2 **Nokha** Ifo mukuphika nokha? — Inde, mkazi wanga adapita kwao.
- 3 **Okha** Kodi muna wapirikitsa? — Iyayi, anachoka okha.

Sometimes it follows the preposition **Pa**: "separately":  
 Ndimagona p ndekha; amuna anga adapita kuulenda.  
 Anyamata akhale pa okha, atsikananso pa okha.

- 1 **Yekha Okha** Ali ndi mwana mmodzi yekha; ena onse anamwalira.
- 2 **Wokha Yokha** Mtedza wokha uli bwino; koma fodya wakanika.
- 3 **Chokha Zokha** Anamanga chipupa chokha, koma sanakhoma denga.
- 4 **Yokha Zokha** Nsima yokha ilipo, koma ndiwo palibe.
- 5 **Lokha Okha** Timapumula loweruka lokha ndinso lamulungu.
- 6 **Wokha Okha** Ulendo woyamba wokha ndinayenda bwino.
- D **Kokha Tokha** Anandipatsa kabuku kamodzi kokha.  
Tinagwira tinsomba tiwiri tokha.

- I **Kokha** Kulemba sindidziwa, koma kuwerenga kokha. (...chabe.) p. 39  
 Ndinadya pang'ono kulawa kokha (...chabe: kungolawa.) p. 49  
 Ndinagwa panjinga kamodzi kokha.

Sometimes it is duplicated: "exclusively", also continuity:

Masiku ano kuli mvula yokhayokha; dzuwa silioneka.  
 Mnyumba mwao mumakhala ndewu yokhayokha.

It is also used with the reflexive form (infix *-dzi-*) p. 76

Anadzipha. He killed himself: Anadzipha yekha.

**Pokha** Inu, musese pakhomo pokha! Anzani adzasesa munyumba.  
 Pano pokha pali mtedza wabwino, koma kwathu kuja wakanika.

**Kokha** Sindinafike ku sitoro koma kumsika kokha.  
 Kuno kokha kunagwa mvula koma kwathu kunalibe.

**Mokha** Musasese muno mokha komanso umu!  
 Umumu mokha muli chimanga; koma umu mulibe.

<b>-mweta udzu, tsekera</b>	<b>-folera nyumba, nkhekwe...</b>
<b>-mata chipupa; mata kalata...</b>	<b>-duka break into 2 pieces</b>
<b>-zula msomali, mtengo</b>	<b>Chingwe chaduka. Njerwa yaduka</b>
<b>-khoma msomali, nsungwi</b>	<b>-khoma msonkho pay the tax</b>
<b>-pachika denga: -khoma denga.</b>	<b>-manga denga</b>

**Demonstrative** They are often joined as suffixes to pronouns and adjectives for greater precision. p. 51

**Ndawerenga** kale bukuli, mundipatse linalo!  
**Chabwino**, tengani ndalama zonsezo. Ine ndisunga zokhazi.  
 Ndalama zimene ndabwera nazo ndi zokhazi. This is the only money...  
 Mkazi wake weniweni ndi woyamba yekhayo.  
 Kodi ndinu amene munabzala mitengo yonseyo?

1. Please, don't speak all together, but one after the other.
2. He has been here for twenty years, and he went home only twice.
3. We rest only on Sunday; the other days we work.
4. These days we eat only beans; can you not prepare some other relish?
5. There are some people who don't eat pork meat; others eat only rice.
6. We all sleep in the same room, but my elder brother sleeps alone.
7. You cannot carry alone that big bundle of firewood. Let me help you!
8. From Monday till Thursday there was no sun, but only rain.
9. In my pocket here there is only one t. left.
10. She has only one son; all her other children are girls.
11. Our house is big; but it has only three rooms. I built it myself.
12. There are rats in all the houses; but there is none in mine.
13. All those oranges are for sale; and the price is 3t each.
14. I have found only one good fruit; all the others are rotten.
15. Were you alone when the accident happened? — Yes, I was alone.

**Provreb:** Anafa kalikongwe nzeru za yekha.

Mwayi	luck, chance	-lemera	be rich; heavy
Tsoka	misfortune	-sauka	be poor; suffer
Umphaŵi	poverty	-pepuka	be light
Usiŵa	shabbiness	-zolowera	get accustomed
Nsanza	rag	-khoza	succeed; do right
Chuma	wealth, riches	-lakwa	do wrong; be mistaken
Mayeso	trial, test, exam	-fotokoza	explain
Khama	stubbornness perserverance	-nyada	be proud

AMENE We come back to this Relative pronoun to see its application to the additional classes of nouns and to the propositions.

"who, which" (subject) : Ana amene anakhoza mayeso ali ndi mwayi. p. 14  
 "whom, which" (object) : Anyamata amene munawaitana sanabwera. p. 26  
 "whose" (possessive) : Kaitaneni anthu amene ana aŵ sali pasukulu. p. 39

It is sometimes dropped, more particularly with Demonstratives:  
 Kodi buku mukuwercngali ndi la yani? — Mwini wake wasoŵa.  
 Kodi mukambukira dzina lake la munthu uŵa tinakomana naye kumsika?

- D. Kamene Mwaika kuti kansaru kaja (kamene) kanali patebulo apo?  
 Timene Timbalame timene tili pawalo apo timadya chiyani?
- I. Kumene Kodi mwakonza chakudya? — Ndili kuphika kumene exactly.
- Famene where Pamudzi pamene timakhala ife pali sitoro ziŵiri.  
 Pamene mukufuna kumanga nyumba yanu ndi pati?  
 when Pamene ndinaŵika kwathu mfumu anandiitana.  
 Pamene munali kuulendo, mkazi wanu anamwalira.
- Kumene where Kumudzi kumene mnzathu anakwatira ndi kwa yani?  
 Sindikudziŵa kumene mng'ono wanga wapita.  
 Kumudzi kumene kwagwa maliro ndi kwa Chimutu.
- Mmene where Tinagona mnyumba mmene munali katundu wambiri.  
 Umu ndi mmene timakonda kucheza kaŵirikawiri.  
 when Mmene tinali kudya nsima, mvula inayamba kugwa.  
 Simuyenera kuseka mmene anzanu ali kuimba nyimbo.  
 how Tiene mmene muphikira ndiwozo! Note suffix -ra p. 81  
 Mundiuze mmene mwachitira! Sindikudziŵa mmene aliri.

Tsiku imene tinamanga ukwati wathu, kunali mvula yokhayokha.  
 Nthawī imene munandiitana, ine krunalibe; ndinali kudambo.  
 Nonsenu mwalakwa, tate wanu, mayi wanu, inu amene. yourself.

AMENEYU This combination of Amene with uyu or uyo constitutes a second form of Demonstratives, with the same meaning "this" or "that". It supposes that the object is being mentioned for the second time: "this" man about whom we are speaking...

- 1 Ameneyu Ameneŵa Kodi ali ndi akazi ena?  
 2 Umenewu Imeneyi — Inde ali nawo koma wamkulu ndi ameneyu.  
 3 Chimenechi Zimenezi Kumudzi kwathu kuli munthu wina dzina lake  
 4 Imeneyi Zimenezi Kalinda. Munthu ameneyo ali wantali zedi.  
 5 Limeneli Ameneŵa Anafuna kuti msonkhano wao ukhale loweruka;  
 6 Umenewu Ameneŵa koma tsiku limenelo kunagwa mvula.  
 D Kameneka Timeneti Kodi kamalaya kaja munagula dzulo ndi aka?  
 I Kumeneku — Inde, ndi kameneka.

Pamenepa Kodi pamene mukufuna kumanga nyumba yanu ndi apa? — Inde, ndi pamenepa. here  
 Kumeneku Tiyeni, tikakhale ku mpandaku!  
 — Iai; kumeneku kuli anthu.  
 Mmenemu Mnyumba umu simugona anthu masiku ano.  
 Ngati simupeza malo kwina, chabwino, mungathe kugona mmenemu.

With uyo we have a similar construction: Ameneyo Amenewo...  
 Kameneko Timeneto: Pamenepo, Kumeneko, Mmenemo there

-li ndi mwayi: -li mwayi: -chita mwayi be lucky  
 -chita khama persevere, be stubborn. Kanthu ndi khama!  
 -khoza mayeso succeed a test. Kulemba sindikhoza (: sindidziŵa)  
 -lakwa mayeso fail: -lephera mayeso: jomba. Cholakwa: a mistake  
 Munthu wolemara rich. Katundu wolemara (different intonation) heavy  
 Mmpħawī: munthu wcsauka, wopanda ndalama.

1. Do you know the time when the accident happened?— It was at noon.
2. I cannot sleep in a house where there is much smoke.
3. There is a burial in the village where you are going.
4. I don't remember how my sister sings that song.
5. Five years ago he was very poor; but now he has become rich.
6. Persevere, don't lose heart; and you will succeed.
7. I hear that you lost your axe. Perhaps it is this one?
8. I don't know where the meeting will take place. Perhaps at Chimutu.
9. At the beginning I suffered much; but now I have got accustomed.
10. She is not lucky. She had three daughters and all of them died.

Proverb: Tsoka sasimba koma mwayi.

Bongo	brain	-vomera	accept, agree
Cholinga	aim	-khulupirira	hope, believe
Ganizo	thought	-ganiza	think
Maloto	dream	-lota	dream
Chizindikiro	sign	-zindikira	recognize
Msalá	madness	-penga	become mad
Khunyu	epilepsy	-dabwa	be astonished
Chitsiru	a fool	-peneka	doubt, hesitate

**YEMWE** This word means "himself", or "the same", "even", "as well". The stem is -mwe; it also takes the Verbal adjective prefix wo-.

- |   |     |        |   |
|---|-----|--------|---|
| 1 | Ine | ndemwe | Ine ndemwe ndikuchita mantha. I myself...               |
| 2 | Iwe | wemwe  | Iwe wemwe umachita ulesi nthawi zina. Kodi si zozna?    |
| 3 | Iye | yemwe  | Asatume muzake, koma abwere iye yemwe (: iye mwini).    |
| 1 | Ife | tomwe  | Ife tomwe tinapita kumsonkhano, chifukwa anatitana.     |
| 2 | Inu | nomwe  | Pegani anzathu, musatiseke chifukwa inu nomwe mwalakwa. |
| 3 | Iwo | omwe   | Akazi ao ali ndi usiwa ndipo iwo omwe amavala nsanza    |

- |   |        |       |   |
|---|--------|-------|---|
| 1 | Yemwe  | Omwe  | Anaba ndalama zonse ndi katundu yemwe: even     |
| 2 | Womwe  | Yomwe | Tinatsiriza kubzala chimanga ndi mtedza womwe.  |
| 3 | Chomwe | Zomwe | Anafentha nyumba, nkhekwe ndi chimbudzi chomwe. |
| 4 | Yomwe  | Zomwe | Anatenga katundu yense ndi mphasa yomwe.        |
| 5 | Lomwe  | Omwe  | Werengani makwacha onse ndi matambbala omwe!    |
| 6 | Womwe  | Omwe  | Ndinamweta tsekera ndi udzu womwe.              |
| D | Komwe  | Tomwe | Kambuku anapha mbuzi zonse ndi tiana tomwe.     |
| I | Komwe  |       | Anaphunzira kuwerenga ndi kulemba komwe.        |

It is often used as a Relative pronoun "the same... who": it puts more emphasis on the identity of the object, excluding any other. **Mundinatse nyale yomwe iri apo!** more precise than **imene**. **Nyumba yomwe khomo lake lilibe chitseko ndi yanga.** **Mumpatse ndalama zomwe muli nazo! (: zimene muli nazo).**

**Pomwe** Amakhala pa mudzi pomwe pali sukulu. on the same spot where Ndinasesa mnyumba ndi pakhomo pomwe. even

**Komwe** Ndikukacheza kumudzi komwe kuli bwenzi langa. where Tinakayenda ku Salima ndi kunyanja komwe. even

**Momwe** Anadzacheza mnyumba momwe timagona ife. where Muyenora kusesa pakhomo ndi mnyumba momwe. even

**Tsiku lomwe anathyoka mwendo tinapita naye kuchipatala.** the very day **Nthawi yomwe tinataluka msukulu mvula inayamba kugwa.** the same moment

...ndi pang'ono pomwe (with a negation): not in the least.

**Alibe mantha ndi pang'ono pomwe.** **Sakumwa ndi pang'ono pomwe.** **Sanaphunzire ndi pang'ono pomwe.** **Sanadye ndi pang'ono pomwe.** **Ndiribe tambala ndi limodzi lomwe:** I don't have a single tambala **Sanapite kwao ndi kamodzi komwe.**

**Monga:** **monga mmene: monga momwe:** as, like, in the same way that: **Chitani monga momwe ndachitira ine.** Note suffix -ra p. 81 **Atsikana a panowa akubvina monga momwe timabvinira ife.** **Kondani anzanu monga momwe ndinakukonderani.**

**YEMWE'YU** In this form of Demonstratives, the Relative yemwe followed by **uyu, uyo** or **uno, uja** re-inforces the identity of an object to the exclusion of any other. "this same...", "that same..."

- |   |           |  |  |
|---|-----------|--|--|
| 1 | Yemweyu   | Omweya   | Alibe katundu wina; ndi yemweyu (:yekhayu)   |
| 2 | Womweyu   | Yomweyi  | Mkeka wanga ndi womweyu.                     |
| 3 | Chomwechi | Zomwechi   | Cholinga changa ndi chomwechi.               |
| 4 | Yemweyi   | Zomwezi  | Teuga nthochi yomweyi; zinazo zili zosapsya. |
| 5 | Lomweli   | Omweya   | Dzina langa laebikhristu ndi lomweli.        |
| 6 | Womweyu   | Omweyu   | Ufa umene ndili nawo ndi womweyu: sukwanira. |
| D | Komweka   | Tomweti  | Kankhuku kaja kadasowa dzana ndi komweka.    |
| I | Komweku   |  | Kulakwa kwanga ndi komweku.                  |
|   | Pomwepa   | Khalani pomwepa, chifukwa palibe malo ena. (: pompa) |  |
|   | Komweku   | Inunso kakhali ku mpanda komweku! (:konku)           |  |
|   | Momwemu   | Leronso tigena momwemu. (: mommu) in this same house |  |

- |   |                 |                     |           |           |                         |
|---|-----------------|---------------------|-----------|-----------|-------------------------|
| 1 | Yemweyo         | Omweyo              | Yemweuno  | Omweano   | Yemwenja Omweaja...etc. |
| D | Komweko         | Tomweto             | Komwekano | Tomwetino | Komwekaja Tomwetija     |
| I | Komweko         |                     | Komwekuno |           | Komwekuja               |
|   | Pomwepo (pompo) | Pomwepano (pompano) |           |           | Pomwepaja (pompaja)     |
|   | Komweko (konko) | Komwekuno (konkuno) |           |           | Komwekuja (konkuja)     |
|   | Momwemo (mommo) | Momwemuno (mommuno) |           |           | Momwemuja (mommuja)     |

**Chomwechi (chenechi)** like this: **Gule ameneyu timavina chonchi.**

**Chomwecho (choncho)** like that: **Chitani choncho!**

**Choncho!** It is like that! Such is life! **Choncho! Titani nanga?**

**Mau anga ndi omwewo.** That is what I wanted to say. (closing a speech)

**Kudandaula kwanga ndi komweko.** **Kulakwa kwano ndi komweko.**



Nkhope	face	-kongola	be beautiful; borrow money
Mfuno	nose	-nun'kha	smell bad, stink
Khungu	skin, blindness	-nunkhira	smell good
Litsiro	dirt	-mina	blow one's nose
Khutu	ear	-gont'ha	be deaf
(pa) khosi	neck	-penya	see, look
Tsitsi	hair	-pesa	comb
N'ebvu	beard	-meta	shave; cut hair

LOCATIVES Here is an exhaustive list of Locatives (see p. 52); it shows the additional note expressed by -mene and -mwe.

WHERE	HERE	THERE		
PA..... Pati?	Pano.....	APA.....	Apo.....	Paja
Pamene		Pamenepa	Panepo	
Pomwe	Pomwepano	Pomwepa	Pomwepo	Pomwepaja
contraction:	Pompano	Pompa	Pompo	Pompaja
KU..... Kuti?	Kuno.....	Uku.....	Umo.....	Kuja
Kumene		Kumeneku	Kumeneko	
Komwe	Komwekuno	Komweku	Komweko	Komwekuja
contraction:	Konkuno	Konku	Konko	Konkuja
MU..... Muti?	Muno.....	Umu.....	Uko.....	Muja
Mmene		Momwemu	Mimenemo	
Momwe	Momwemunu	Mimenemu	Momwemo	Momwemuja
contraction:	Mommuno	Mommu	Mommo	Mommuja

PATI? on which spot? Ndikhale pati? Kalata ili pati?

Pamene on the spot where... Kodi mwaona pamene adamanga nyumba yake?

Pomwe on the same spot where... Khalani pomwe pali anzanu!

Fano on this spot where I am... Ine pamudzi pathu ndi pano.

Pompano on this same spot... Mkazi wanganso pao ndi pompano.

Apa on this spot near Pamene mukufuna kumanga nyumba ndi apa?

Pamenepa (2nd mention) — Inde, ndi pamenepa.

Pomwepa on the same spot Nkhokwe yanganso idzakhala pomwepa.

Apo on that spot there Ndipo khola langa lidzakhala apo.

Panepo (2nd mention) Kale pamenepo panali nkhalango.

Pomwepo on that same spot Mfumunso khola lao lidzakhala pomwepo.

Paja on "the" spot, you know which Pepani, n'fasiya buku pampano paja.

Leronso paga marilo pamudzi pompaja.

KUTI? at, in, to which place? Mumakhala kuti? Akupita kuti?

Kumene at, in, to place where... Sakud'iswa kumene mnrake wapita.

Komwe at, in, to the same place where... Kasewerani komwe kuli anzanu.

Kuno at, in, to this place where I am Bwerani kuno! Kuno kali njala.

Konkuno at, in, to this place... Iyenso adzakwatira konkuno.

Uku at, in, to this place near Anzanu ali kucheza kumpanda uku.

Kumeneku (2nd mention) Kumeneku kuli malo abwino, zooka.

Komweku at, in, to this place Inenso ndikacheza nawo komweku.

Uko at, in, to that place there Ku mudzi uko ndi kwa Chimutu.

Kumeneko (2nd mention) Ndinapita kumeneko dzulo; kunali maliro.

Kuja at, in, to "the" place, you know which Kumudzi kwao kuja ndi kuti?

Konkuja at, in, to "the" same place Leronso akupita kumudzi konkuja.

MUTI? in which room? Nditsire muti chimangachi, umu kapena umu?

M'mene in the room where... Mnyumba m'mene muli makoswe ambiri ndi umu.

Momwe in the same room where... Kalata ili m'dengu momwe muli mabuku.

Muno in this room where I am Ine ndimagona mnyumba muno.

Mommuno in this same room... Mng'ono wanga iyenso amagona mommuno.

Umu in this room near Mkulu wanga amagona umu; amagona pa yekha.

M'menemu (2nd mention) Chabwino; mungathe kuika katundu wanu m'menemu.

Momwemu in this same room Njinga yanunso ikhale momwemu!

Umo in that room there Umo simugona anthu; chifukwa muli katundu wambiri.

M'menemo (2nd mention) Mphasa, madengu, makasu, zonse zili m'menemo.

Momwemo in that same room Ng'omanso imakhala momwemo.

Muja in "the" room; you know which Ndaiwala chipewa mnyumba muja.

Mommuja in "the" same room Leronso tigona m'nyumba mommuja.

Some words may have still another meaning according to context:

Pamenepa : Mnamanya mkazi wanu. Pamenepa mwalakwa? On this point.

Alendo aja sabwera. Pamenepa titani? In this case...

Pompo : Ndinatola mwala; pompo garu anathawa. (:nthawi yomweyo)

Ngati wana adwala, pitani naye pompo ku chipatala! at once

Momwemo ! Mscnkhanu wakanika chifukwa cha mvula. Momwemo! (:Choncho)

Ngati male palibe, momwemo, ndikagona kwina. Such is life!

Mommuja : Matenda aja ali bwanji? — Mommuja. as before, no change.

Kodi adakonza njinga yanu? — Ai, ili mommuja.

Proverb: Fodya ndi yemwe ali pamfuno.

(pa) Kamwa	mouth	-yasama	open mouth; yamw
(m') Mero	throat	-meza	swallow
Mlomo	lip	-yamwa	suck breast
Lilime	tongue	-seteka	lick
Dzino (pl. Mano)	tooth	-tafuna	chew
Malobvu	spittle	-ledzera	be drunk
Magazi	blood	-labvula	spit
Mimba 4	belly	-sanza	vomit

**KUTERE** is a verb related to **Kuti**, it means "say this"; "do like this".  
**Ife timatere** (: **timachita chonchi**). **Mutere!** (: **Chitani chonchi**).  
**Gule ameneyu kubvina kwake timatere.**  
**Mawu anga nditere** (: **Mawu anga ndi awa**).

**KUTERO** is a similar verb meaning "say that", "do like that".  
**Teroni!** (: **Chitan, choncho!**) **Musatero!**  
**Anatero kulankhula kwake** (: **Kuyankha kwake ndi kumene'ko**).  
**Kutero'ko ndi kulakwa.** It is wrong to say that, or do like that.  
 Both are also used as verbal adjectives "like this", "like that":  
**Anagula njinga yotere** (: **yonga iyi** or also **yoti chonchi**)  
**Ndinani ndi nkaku yotero** (: **yonga iyi** or **yoti choncho**).

**Locatives** The demonstratives "here", "there" **apa apo; uku uko; umu umo** are often joined as suffixes to other words such as:

<b>Penapa</b>	<b>Penapo</b> : <b>Kwinako</b>	<b>Kwinaku</b> : <b>Mwinamu</b>	<b>Mwinamo</b>
<b>Ponsepa</b>	<b>Pensepo</b> : <b>Konseku</b>	<b>Konseko</b> : <b>Monsemu</b>	<b>Monsemo</b>
<b>Pokhapa</b>	<b>Pokhapo</b> : <b>Kokhaku</b>	<b>Kokhako</b> : <b>Mokhamu</b>	<b>Mokhamo</b>

They can be joined also to various adverbs such as: p. 25

<b>Pamwambapaja</b>	<b>Pamwambapo.</b>	<b>Kumwambaku</b>	<b>Kumwambako.</b>	<b>Mmwambamu.</b>
<b>Pansipa</b>	<b>Pansipo.</b>	<b>Kunsiku</b>	<b>Kunsiko.</b>	<b>Munsimu.</b>

Joined to a verb, it is always the form -po -ko -mo p. 53

**Ndipo** : **Apa ndipo** (pamene) **pali dothi labwino.** It is here that...  
**Pa February ndipo** (pamene) **pamagwa mvula yambiri.** It is... that  
**Ndiko** : **Kuchipatala ndiko** (kumene) **timapeza mankhwala abwino.**  
**Kwa Chimutu ndiko** (kumene) **tidzapanga msonkhano wathu.**  
**Ndimu** : **M'sitiro umo ndimo** (mmene) **muli zinthu zambiri zamalonda.**  
**Madzulo ano ndimo** (mmene) **tidzacheza nawo alendo aja.**  
**Umu ndimo** (m'mene) **timachitira.** This is how we do.

**Pa Ku Mu** There are some nouns which usually take a preposition; for instance certain parts of the body:

**Tsekani pakamwa!** Close your mouth! **Pa khesi panga patupa.**  
**M'mero mwanga mwauma.** **M'maso mwanga mwada.**

**MANNER** Most of the adverbs of manner are found with nouns and the preposition **mwa** or with verbs and the prefix **mo-**:

<b>Mwaulesi lazily</b> : <b>ndi ulesi.</b>	<b>Mwamphamvu vigorously</b> : <b>kwa...</b>
<b>Mwamsanga quickly</b> : <b>msanga</b>	<b>Mwachipongwe insolently</b>
<b>Mwaulemu politely</b>	<b>Mwaululu freely, generously</b>
<b>Mwamwayi fortunately</b>	<b>Mwatsoka unfortunately</b>
<b>Mwangozi by accident</b>	<b>Mwachitsanzo for example</b>
<b>Mothamanga speedily</b>	<b>Mosafulumira without any haste</b>
<b>Monyada proudly</b>	<b>Mopeneka doubtfully</b>

**Anandiyankha mopanda ulemu, impolitely**  
**Anatotozoka nkhani yake modandaula ndithu.**  
**Dikirani pang'ono; abwera posachedwa, soon**  
**Mvula ibwera madzulo posapeneka, without any doubt**

There are also adverbs expressing motion, position or direction; they take the prefix **cha-** or **cho-** (verbs):

<b>-Yenda chambali</b> sideways	<b>-gona cham'mbali</b> on the side
<b>-yenda cham'mbuyo</b> backwards	<b>-penya cham'mwaraba</b> upwards
<b>-yenda chowerama</b> stooping	<b>-yenda chokwawa</b> crawling: <b>mokwawa</b>
<b>-khala chogwada</b> kneeling	<b>khala choimirira</b> standing: <b>chiriri</b>

Some other adverbs:

**chagada** on the back; **fufumimba** on the belly **-gona...**  
**daia** purposely, intentionally; **Dere** (: **chonchi**) **Dero** (: **choncho**)  
**Bwino** well; **Ali bwino masiku ano.** **Amadziwa bwino Chichewa.**  
 carefully: **Mangani bwino katunda!** **Tsekani bwino chirona!**  
 gently: **Yendetsani njinga bwinobwino!** duplicated  
 be careful! **Bwino, apa pali dzenje!** (: **Cheujerani!** **Basopo!**)  
**Bwinotu, garuyo amaluma.** (p. 94)

later, another time: **Kapumuleni pang'ono; tidzacheza bwino.**

**Siyani katundu wanu pompano!** **Mudzatenga bwino.**  
**Bwinopo** rather well: **Anadwala matenda akulu; koma tsopano ali bwinopo.**  
 The suffix **-po** here means **pang'ono**; **Ali wamkulupo** rather p. 95

Proverb: **Tsoka silinunkha**

Nyengo	season	-otha moto	warm oneself near fire
Nyenyezi	star	-othera dzuwa	" " in the sun
Mtambo	cloud	kongwa	be seized with cold
Dontho	drop	-bvumbwa	be wet with the rain
Mphezi	lighting	-dontha	leak, drip
Lume	dew	-waza	sprinkle, drizzle
Utawaleza	rainbow	-nyowa	be wet, soaked
Liwiwo	speed	-thamanga	run

INFIXES Up to now we have seen the following verbal Infixes:

-ku-	present continuous (contraction) p. 9 Akuceza ndi yani! habit (monosyllabic verb and negation) p. 18 Moŵa sakumwa.
-an-	past p. 22 Mnzanga uja anapita kwao dzana.
-da-	past p. 22 Ndili ndekha; mkazi wanga adapita kwao.
-dza-	future p. 22 Musavutike! Tidzakuitanani... motion "come and do" p. 44 Tadzakuonani. Dzasonkheni moto!
-ka-	motion "go and do" p. 44 Akukasamba kudambo. Katoleni nkhuini!
-ma-	habit p. 18 Ndimakomana naye nthawi zina kumsika.
-a-	perfect p. 30 Pepani, mwasochera. Mvula yakanika.
-ngo-	just p. 49 Uyu amangokhala, safuna kuthandiza anzake.

WHEN? Considering the relation of priority (time) between two facts we find three possibilities: one fact may take place "before" the other, or at the same time "during", or "after" the other.

-SANA- infix (sa negation; na past) indicates that the fact took place "before" another, the other was "not yet" performed;  
Mwana anamwalira dzuwa lisanalowe... before sunset. (Note -E)  
Tinafika kwathu dzuwa lisanatuluke... before sunrise.

-LIKU- This is the Present Continuous "at the same time, during" relation or simultaneity; concomitance. (Note the present)  
Timaweruka ntchito dzuwa lili kuloŵa... at sunset.  
Adanyamuka dzulo dzuwa lili kutuluka... at sunrise.

-TA- infix indicates that the fact took place "after" another, the other having "already" taken place.  
Anamwalira madzulo dzuwa litaloŵa... after sunset.  
Tinapita ku sukulu dzuwa litatuluka... after sunrise.  
Ndidzakulipirani mutamaliza ntchito yanu.  
Alendo a'a asanafike muyenera kusesa bwino m'nyumba umu.

Kwacha it is dawn : Kusanache before dawn : Kutacha after dawn.  
Kwada it is dark : Kusanade before dark : Kutada it was already dark.  
Tambala woyamba at first cockcrow. Tambala asanalire. ...atalira.

Ndinafika kwathu anthu asanagone. ...atagona.  
Anadzaloŵa m'nyumba mwathu, ife tili m'tulo, osazindikira kanthu.  
Ndinapeza mzunga ali kuotha moto. ...ali kusoka mphasa.  
Ndinapeza mphunzitsi palibe absent. Ndinampeza atachoka.  
Ndinampeza ali moyo alive. ...atafa dead. ...ali gone. ...ali tsonga.

...AGO : Kwapita zaka zingati? : Papita zaka zingati? see p. 30  
Mwana wake anatha msinkhu kwapita zaka ziwiri.  
Kalekale long ago. Kwapita nthawi yaitali.

AFTER : Itapita miyezi itatu: Patapita miyezi itatu after 3 months.  
Anabadwa loweruka ndipo atapita masiku anayi anamwalira. p. 30  
Tidzapanga wina msonkhano patapita milungu iwiri.

FIRST : Note the construction -yamba followed by the Perfect tense:  
Muyambe mwakonza njinga! First repair the bicycle.  
Sindinyamuka msanga; ndiyamba ndadya nsima. (: Poyamba ndidya)  
Tiyambe tawerenga ndalama! : Tiwerenge ndalama choyamba!

PO- prefix (pa ku-) in front of a verb is the equivalent of a preposition "on, in by doing something" or "when...": present participle.  
It supposes that the subject is the same in the two clauses.

Tidzaimanso pompano pobwera on our way back.  
Timayenda limodzi popita kusukulu. Kodi umapemphera pogona?  
Anapweteka dzanja pokonza njinga. Timatola nzeru pakutani?  
Pobwera kuulendo anadzapeza mkazi wake ali ndi mwamuna wina.  
Munalakwa posaitana mafumu kumsonkhano; adzayesa chipongwe.

1. On my way to the market I met many women going to the burial.
2. After the death of my father, my mother married another man.
3. Before sweeping, you must sprinkle some water on the floor.
4. If you want me to help you; first do what I have told you!
5. Go and pick up some firewood before the rain starts!
6. We like to warm ourselves in the sun before starting our work.
7. What did you answer when the chief asked you your name?

Proverb: Tambala akavumbwa alibe malonda.

Boma	Government	-weruza	judge, admonish
Msonkho	tax	-lola	allow, permit
Ufulu	freedom, generosity	-letsa	forbid, hinder
Ukapolo	slavery	-umiriza	urge, compel
Khelo	ancestor	-simba	report, narrate
Mpingo	assembly, Church	-landa	seize, take, snatch, steal
Ndende	prison, jail	-langa	punish, admonish, instruct
Mbiri	report, fame	-pulumutsa	save, deliver

CONDITIONAL The word ngati "if" expresses a present condition; it is the only construction possible with -li "be, have":

Asapite kumsonkhano ngati sali bwino! Sindidziwa ngati alipo.  
Pitani kwanu ngati mulibe mawu! Musaiowe ngati mulibe anthu!

-KA- infix expresses a future condition or possibility "if" or "when":  
Akabwera alendo, mudzandiuze. Ukavutanso galu adzakuluma.  
Mukapita kuchipatala msanga, mwina mudzachira.  
Ndizabweza ndalama zija ndikadzagulitsa mtedza. when I have sold

Negation: instead of the prefix si-, we use the verb -panda followed by the Infinitive. Sometimes also the verb -leka.

Alendo aja akapanda kubwera, mudzandiuze.  
Mukapanda kupita kuchipatala, mwina simudzachira.  
Ndikapanda kumuitana, sadzabwera.

-KADA- infix expresses either a supposition or a conditional, or an unfulfilled wish, a regret. The infix is repeated twice:

Mukadapita kuchipatala, mukadachira msanga. ...you would have...  
Ndikadamuitana, akadabwera. If I had called him, he would have...  
Alendo aja akadabwera, ndikadakuuzani.

Negation: instead of the prefix si- we use the verb -panda.

Mudakapanda kupita kuchipatala simudakachira. If you had not gone...  
Ndikadapanda kumuitana, sakadabwera.

Mukadandiura msanga! If only you had told me immediately!  
Ndikadakhocha mayeso! unexpressed ndikadachita mwayi.  
Ndikadapita kumaliro, koma mfumu anandituma kwina kwake.

Pang'ono ndikadagunda mtengo. I nearly bumped into a tree.  
Muchenjere naye galuyo! Pang'ono akadandluma.

Here are other various constructions equivalent to -kada-:

-kana- infix: Ndikanapita kutchalitchi, koma ndinali ndi usiwa.  
Akanayesanso kachiwiri, kapena akanakhoza.

-daka- infix: Adakalima fodya, adakapeza ndalama zambiri.  
However -daka- infix may have two other meanings: see context.  
motion: Adakalima fodya. He went to cultivate... p. 44  
"still" Adakalima fodya. He still cultivates tobacco. p. 75

bwenzi is a word which just introduces the second part of the sentence, it expresses a consequence and can be translated by "well...":  
Mukadapita kuchipatala, bwenzi mukadachira msanga.

-ta- infix can be used instead of -kada- after the word bwenzi:  
Mukadapita kuchipatala, bwenzi mutachira msanga.  
Alendo aja akadabwera, bwenzi nditakuuzani.

-chi- infix can be used instead of the first -kada-:  
Muchihipita kuchipatala msanga, bwenzi muli bwino lero.  
Ndichidziwa dzina lake la munthu'yo ndikadakuuzani.  
Other constructions: Akhala...: Kuchikhala kuti...: -kada-

Akhala mwapita kuchipatala, bwenzi mukadachira posachedwa.  
Kuchikhala kuti mkaziyo ali wosakwatiwa, bwenzi nditamkwatira kale.

Mukadapanda kupita kuchipatala, si bwenzi muli moyo lero.  
Ndikadapanda kumuitana, si bwenzi atabwera kuno.  
Pakadapanda bambo ndi mayi wanu, simukadabadwa.  
Mayi wako akadzamwalira, adzakusamala ndani?

Nyumba ya Malamulo Legislative House. Akupita ku Boma (offices)  
Kapolo slave. Makolo ancestors, parents. -Shoma msonkho pay tax.  
Akulu a Boma officials. Akulu a mpingo Church elders.  
Alibe mbiri yabwino good reputation. Mbiri yakale Old Testament.  
Mbiri ya Achewa history. Timamva mbiri yomweyo posepense rumour.  
Mwina makolo amaletsa ana kuti asapite kusu'kulu. (note infix -sa-)  
Makolo anga salola kuti ndikwatiwe naye manyamatayo.  
Mulungu achileka kutsamala, si bwenzi tili moyo anthufe.  
Mukapanda kuiweruza nkhaniyo, tipita nayo kubwalo.  
Kumudzi kalikonse kumene ndimafika ndiramva mbiri yokhayokhayo.  
Ndikapanda kuma ntha'wi yomweyo, ndikadagwa mudzenie.  
Adakapanda kumiriza mwana waoyo, si bwenzi iye akadakwatiwa.  
Anandilanda munda, ndipo tsopano ndikusowa pelima.

Proverb: Patsepatsa nkulanda; mwana wa mfulu apatsa yekha.

<b>Chibwenzi</b>	friendship	<b>-lonjeza</b>	promise
<b>Chipangano</b>	agreement, contract	<b>-pangana</b>	agree, make contract
<b>Mbeta</b>	unmarried woman; free	<b>-funsira</b>	ask in marriage
<b>Chiwongo</b>	dowry	<b>-tula</b>	put down a load
<b>Nkhoswe</b>	tutor, advocate	<b>-yendera</b>	visit
<b>Mpongozi</b>	mother-in-law	<b>-lekana</b>	separate
<b>Mkamwini</b>	son-in-law	<b>-sudzula</b>	divorce
<b>Mtsibweni</b>	uncle (maternal)	<b>-senza</b>	carry on the head

**-NGA-** infix is a Subjunctive form (last vowel is always **-e**). It expresses a permission, a possibility or supposition.

"may" permission: **Ndingakuthandizeni? May I help you?**  
**Tingalowe? Ndingabwereke njinga yanu?**

"can" possibility: **Kodi mungandithandize pang'ono? (interrogation)**  
**Sanganame. Simungadziwe dzina lake. (negation)**

"not yet" with a negation: **Sangabwere: Sanabwerebe see p. 75**  
So we may have two different meanings according to context and intonation: **Sangabwere** He cannot come. He won't come: **Sabwera.**

"lest, in case": to prevent some occurrence: (**kuti** is often dropped)  
**Thawani msanga (kuti) garu angakulumeni.**  
**Musasewere ndi mpeni, mungapweteke mzanu.**  
**Yendetsani bwino njinga, mungagunde mtengo.**

"even if, though" supposition: **Nyumba ingagwe, palibe kanthu.**  
**Angandiitane kumsonkhano, sindipita.**

**-ngakhale** has the same meaning "even if, although": various constructions:  
**Ndingakhale ndidwale, palibe kanthu.** Even if... (supposition).  
**Ndingakhale ndili kudwala, sindidandaula.** Though I am... (a fact).  
**Ngakhale ndili kudwala sindidandaula.** **Ngakhale** as a conjunction.  
**Ngakhale... ngakhale... whether... or... either... or...:**  
**Onse ali okondwa, angakhale abambo, angakhale amai.**

**-ngathe** "can" subjunctive form is more common than the present form **-tha** which expresses more a physical ability:

**Ngati mulibe mawu ena, chabwino, mungathe kupita kwanu.** also **khoza**  
**Mungathe kudandaula: Mukhoza kudandaula.**  
**Sinditha kuyenda, ndatupa miyendo. Kodi muitha ntchito imeneyo?**  
**-tha** also means "finish" or "be finished":  
**Kodi mwatha? (mwatsiriza: mwamaliza), Msonkhano watha.**

Other constructions with the infix **-nga** and **chotani** or **bwanji?**

**Atendo angachuluke chotani, onse adzapeza malo.** However numerous...  
**Ndingasauke chotani, sindidandaula.** However much I may suffer...  
**Ndingadandaula bwanji, safuna kundithandiza.** also **chotani** or **motani**  
**Kungatanikungatani, ndikwatira mtsikana ameneyo.** Whatever may happen

**STILL** is translated by the suffix **-be** or the infix **-daka-** or both; we cannot use the suffix **-be** with the verb **-li** because it would mean "have not" **-libe.**

**-be** **Mwana ali kulirabe (: akulirabe)** is still crying.  
**Kodi mumapitabe kusukulu? Muyenera kuphunzirabe.**

**-daka-** **Adakadandaula** She still complains. **-daka-** has also other meanings:  
**Adakadandaula (past conditional)** If she had complained... p. 73  
**Adakadandaula kwa mfumu (motion past)** She went to complain  
**Adakali wamng'ono** He is still small. **Adakali mnyamatabe.** p. 44  
But **Alibe mwana** she has no child. **Adakalibe mwana** no child yet.

**-daka-be** **Adakadandaulabe** she still complains. **Adakalirabe.**  
**Adakali wamng'onobe, Adakali mnyamatabe.**

**-ka-** infix with the verb **-li** can also mean "still", usually it expresses a past "when I was...":

**Mukali mnyamata (: Mukadali mnyamata)** you are still young.  
**Pakali pano sukulu ikuyenda bwino.** Up to now... (...**idakayenda**)  
**Mayi wanga anamwalira ndikali wamng'ono (: ...ndili wamng'ono)**  
**Ndikali mnyamata, ndinkapita ku sukulu masiku onse.**

**NOT YET** is also translated by the suffix **-be;** or the infix **-nga-:**  
**Sanafikebe** he has not yet arrived. (: **Sangafike** p. 74)  
**Sanadzukebe (: Sangadzuke).** **Sangakwatiwe (: sanakwatiwebe).**  
**Mwana adakalibe mano (: sangamere mano)** has no teeth yet.

**chi-re** is another construction meaning "still", for a few verbs:  
**Mai ali chigonere (: adakagonabe)** is still in bed.  
**Mfumu ali chidwalire (: adakadwalabe)** is still sick.

**-pala ubwenzi: -panga chibwenzi: -palana chibwenzi** make friendship  
**-funsira mbeta** ask in marriage. **Mbeta** unmarried girl or woman, free  
**Mbeta yakanika** the tractations between the two family groups have failed.  
**Mbeta yatha** both parties have come to an agreement; the girl is promised.  
**-tula mbeta** introduction of the boy to the girl's village.

Proverb: **Mkamwini asamakule mwendo.**

Chikondi	love	-dana	hate one another
Chidani	hatred	-yanjana	be reconciled
Mnansi	neighbour	-nyenga	cheat, deceive
Mbala	thief	-chimwa	sin; do wrong
Chigololo	adultery	-sinjirira	calumniate
Mitala	bigamy	-tsutsa	argue, refute
Umboni	testimony	-pepesa	apologize
Tambwali	unreliable man	-khululukira	forgive

-DZI- infix is a reflexive "oneself"; it supposes that the action is done intentionally. The pronoun *yekha* is sometimes added. p. 60  
Anadzipha (*yekha*) He killed himself (suicide).

Anadzimanga pa mtengo; Anadzipachika pa mtengo.  
Amadzitchula mphunzitsi, koma sanaphunzire konse.

-NKA- (also -KA-) "used to": equivalent of -MA- is the past tense.  
Chaka chatha ankapita kusukulu, koma chaka chimo amangokhala.  
Kale anakonda kukasaka nyama, koma tsopano wakalamba.  
Kodi kale ku Malaŵi kuno anthu ankavala zotani?

-BA- "meanwhile": invitation to carry on an action while another is in progress: Mphunzitsi sangafike. Tibakaseŵera.  
Badikirani pang'ono! Ndiŵera tsopano apa.  
Bapumulani m'nyumba umu! Ine ndiyamba ndasamba m'maso.  
Zikomo akulu, bagwirani ntchitoyo! Ine ndapita.

-ZI- "must": express a strong obligation equivalent to an order.  
Munthuyo azipita kwao. (:...apite kwao!)  
Anthufe tisangokhala; tizigwira ntchito kuti dziko likwere.  
It also expresses a consequence (future), or a possibility (in questions):  
Njinga yanga yafa. Momwemo; tizingoyenda pansi.  
Anthuŵa gule wao wakanika. Tiyeni, tizipita kwathu.  
Ndiziyankha chiyani? Kodi ndizitero masiku onse?  
After kuti it can also be used instead of the Subjunctive:  
Mumuze kuti azipita kwao (: kuti apite kwao).  
Muŵapatse mpira anaŵa kuti aziseŵera nawo. (: kuti aseŵere nawo).

-MA- expresses a habit p. 18; or, sometimes, a recent past (intonation):  
Munali kuti? — Timacheza m'nyumbamo (: tinali kucheza).  
Wachoka tsopano apa. Amasoka mphasa pa bwalopo (anali kusoka).

-TA- means "after" p. 70; or is the equivalent of -kada- p. 73; or also expresses a wish: Nditaona! Let me see! Nditayesapo ine!  
Nditakufunsani chinthu chimodzi! Ita'khala yanga njinga imeneyo!

ORDERS are expressed by the Imperative or the Subjunctive:  
Pita! Pitani! Idya! Idyani! prefix *i-* in monosyllabics  
Upite! Mupite! Udye! Mudyeye! subjunct. (wish, command)  
Usapite! Musapite! Usadye! Msadyeye! infix *-sa* negation.

Another negative form: Osadya! Osapita! more colloquial; it is an invitation to stop an action which has started:

Usalankhule! Don't start speaking! Osalankhula! Stop speaking!  
Musadye nthochizo! Osadya nthochizo!

With an object-pronoun infix, we always find the Subjunctive; there are three forms: the subject prefix and object infix can be dropped:

Mundipatse mpeni! Ndipatseni mpeni! Patseni mpeni! Give me the knife.  
Mumpatse mpeni! Mpatseni mpeni! Patseni mpeni! Give him...

Note the difference between Patseni! "to me"; Patsani! "to him".

To soften an order, in some areas we find the suffix *-ko*:

Patseniko! or Patsenkoni! Give me some please! (a portion)  
Patsaniko! or Patsankeni! Give him some! Lawaniko! Taste it!  
Kwezeniko! or Kwezenkoni! Give me a lift! (car, bicycle...)  
Gwireniko! or Gwirenkoni! ndingagwe. Hold me, lest I fall.  
-in suffix is sometimes postponed: Nyale iri apo; bweera nayoni!

The command or wish can be re-inforced, soften or modified by the various infixes mentioned in the previous lessons:

Ka- motion "go and do" p. 44: Kaitane mu-ako! Kapaleni moto!  
sometimes a future: Mukabwerenso maŵa!

Dza- motion "go and do" p. 44: Dzasonkhe moto! Dzatsukoni mbale!  
sometimes a future negative: Musadzauza anthu ena!

Ma- habit, negation: Musamaŵgokhala! Usamachite zopasa!  
Osamalankhula m'nyumba muno!

Ta- re-inforces, invitation to do what is expected to be done:  
Tayesani! Have a try (since you wanted to try).  
Tapita! Tamverani! Tayankhani! Talankhulani!

Ba- "meanwhile" p. 76 : Dzuŵa libalipo; mubakap'nyanya mpira pakhomo!  
Eatherani dzuŵa pompano! Ine ndikaitana mphunzitsi.

Ngo- "just" p. 49: Ingobwerani! Tangobwerani!

Zi- obligation p. 76: Ziŵerengani! Kaziŵerengani!

Mpongori akundida...hate me: ...adana naye. Udani: Chidani.

Mdani enemy. -chita mitala take a second wife: -tenga chiŵiri.

Proverb: Fisi adalira msampha utaning'a

<b>Mthenga</b>	message	<b>-kamba</b>	tell, narrate
<b>Phokoso</b>	noise, tumult	<b>-sokosa</b>	make noise, disturb
<b>Chilankhulo</b>	language	<b>-tonthola</b>	be silent
<b>Chinsinsi</b>	a secret	<b>-ulula</b>	disclose, reveal
<b>Fanizo</b>	parable, comparison	<b>-lalika</b>	proclaim
<b>Mwambi</b>	proverb	<b>-tanthauza</b>	mean, signify
<b>Mwambo</b>	custom, rite	<b>-tamanda</b>	praise
<b>Nthano</b>	tale, fable	<b>-tukwana</b>	insult

SUFFIXES We have already met one verbal suffix **-NA** p. 49; it expresses reciprocity: **-kondana** love one another; **-komana** meet

**-TSA** is another suffix which has a causative meaning: to make someone do something, or to get something done:

**-cnetisa: Mundionetse chithunzi!** Let me see, show me...

**-zimitisa: Zimitisani nyale!** Blow out the lamp!

There are two forms **-etsa** or **-itsa**: the last vowel **-a** of the stem changes into **-e** (**-etsa**) or **-i** (**-itsa**) according to the second last vowel. If it is

**A I U** we must use the form **-itsa**

<b>-thawa:</b>	<b>-thawitsa.</b>	<b>-wala</b>	<b>-walitsa</b>	<b>-dabwa:</b>	<b>-dabwitsa</b>
<b>-funsu:</b>	<b>-funsitsa.</b>	<b>-imba</b>	<b>-imbitsa.</b>	<b>-chira:</b>	<b>-chiritsa.</b>
<b>-dziwa:</b>	<b>-dziwitsa.</b>	<b>-zula:</b>	<b>-zulitsa.</b>	<b>-sunga:</b>	<b>-sungitsa.</b>

**O E** and monosyllabic verbs: we must use the form **-etsa**:

<b>-konza:</b>	<b>-konzetsa.</b>	<b>-topa:</b>	<b>-topetsa.</b>	<b>-soka:</b>	<b>-soketsa</b>
<b>-penya:</b>	<b>-penyetsa.</b>	<b>-seka:</b>	<b>-seketsa.</b>	<b>-yera:</b>	<b>-yeretsa.</b>
<b>-gwa:</b>	<b>-gwetsa.</b>	<b>-dya:</b>	<b>-dyetsa.</b>	<b>-tha:</b>	<b>-thetsa.</b>

With that suffix we can make new verbs:

<b>-chulukitsa</b>	multiply .	<b>-chepetsa</b>	diminish .	<b>-yamwitsa</b>	breast-feed
<b>-talikitsa</b>	lengthen .	<b>-fupikitsa</b>	shorten .	<b>-kullitsa</b>	enlarge
<b>-kondwetsa</b>	rejoice .	<b>-lekanitsa</b>	separate .	<b>-fewetsa</b>	soften

Some verbs have a contracted form (many verbs ending with **-ka**) :

<b>-choka</b>	: <b>-chotsa</b>	(instead of <b>-choketsa</b> )	<b>-tuluka</b>	: <b>-tulutsa</b>	
<b>-tsika</b>	: <b>-tsitsa</b>	<b>-leka</b>	: <b>-letsa</b>	<b>-sauka</b>	: <b>-sautsa</b>

Some verbs have a soft form **-za** instead of **-tsa**; or both :

<b>-kwera</b>	: <b>-kweza</b>	<b>-tuma</b>	: <b>-tumiza</b>	<b>pereka</b>	: <b>-perekeza</b>
<b>-lowa</b>	: <b>-lowetsa</b>	<b>-loweza</b>	<b>-chira</b>	: <b>-chiritsa</b>	: <b>-chiza</b>
<b>-bwera</b>	: <b>-bweretsa</b>	<b>-bweza</b>	<b>-chenjera</b>	: <b>-chenjeretsa</b>	: <b>-chenjezo</b>

The two forms **-tsa** and **-za** may have different meanings.

--Tsa suffix sometimes conveys a notion of intensity in the action, or superlative "much", "too much"; according to the context and intonation: see the difference between the following examples.

**Gwiritsani chingwe!** Hold the string firmly **Muwagwiritse ntchito!**  
**Mwanayu wadyetsa...** has eaten much, too much. **Mayi akudyetsa mwana feed.**  
**Tiyeni anyamata, imbitsani!** ...vigorously! **Imbitsani anyamata!**  
**Munthu woseketsa** a man who likes to laugh. **Anatiseketsa.**

Some verbs can take a reduplicated suffix to express intensity:

<b>-penya</b>	: <b>-penyetsa</b>	: <b>-penyetsetsa</b>	look carefully, attentively.
<b>-yang'ana</b>	: <b>-yang'anitsa</b>	: <b>-yang'anitsitsa</b>	look carefully.
<b>-ona</b>	: <b>-cnetisa</b>	: <b>-onetsetsa</b>	look carefully.
<b>-funa</b>	: <b>-funitsa</b>	: <b>-funitsitsa</b>	desire ardently.
<b>-mva</b>	: <b>-mvetsa</b>	: <b>-mvetsetsa</b>	understand well.

**Kadziwitzeni mphunzitsi kuti mwana wake akudwala.** inform  
**Anyamatawa sayenera kumangokhala; chifukwa chiyani simuwagwiritsa ntchito?**  
**Ana inu, fulamirani! Mukundichedwetsa.** Taonani, **dzuwa liri kulwa.**  
**Inu, kaphitani nsima!** He tibachezetsa alendowa, keep company  
**ineno ndimafunitsitsa kuphunzira nao chizungu; koma sindipeza nthawi.**  
**Mi nali kuti? — Ndimacheza naye mnzanga uja.** Nkhani zake zinali zoseketsa.  
**Zikomo, nawachita bwino kundikumbutsa nkhan'yo.** Ndikadawala, remind  
**Musachulikitse mawu pokamba nkhan'i.** Inali ntchito yotopetsa, tiring  
**Anadzamangitsa ukwati wao ku tchalitshi konkuno, dzanal.**  
**Ndinaitantsa mabuku ku Blantyre order.** Inali nkhan'i yochititsa manyazi.  
**Ndikufuna kuikiza ndalama kuti (: sung'za) ... in deposit.**  
**Mukundichititsa mantha frighten.** Zinali zomvetsa chisoni cause pity.  
**Adakonzetsa njinga yake ku Lilongwe.** Imbitsani galimoto! stop  
**Mvula inagwa yambiri usiku ndipo tsopano madzi alekeza umu.** reach  
**Kaphitseni madzi!** boil (tr.). **Bwinota, mungagwetse mwana!**  
**Pepani, sindikhalitsa stay long; ndinyamukanso posachedwa.**  
**Mwanayu sali bwino iyayi; dzamdrutsemi ndipo mupite naye ku chipatala.**  
**Mnzanu uja akubisa mawu.** Muyenere kumfunsitsa ndithu, mpaka aulule.  
**Fasi, tafika.** **Muyambe mwatsitsa katundu!** **Mundiperekeze kwa mfuma!**  
**Ndinaona chinthu chedabwitsa surprising.** **Anatinamiza badda tell lie.**

<b>-Chiritsa</b>	munthu cure a man	: <b>-chiza</b>	n'henda cure a disease
<b>-lowetsa</b>	mbuzi m'khola	: <b>loweza</b>	mawu memorize, study
<b>Ulesi</b>	umabweretsa umphawi	: <b>-bwereza</b>	repeat; <b>-bweza</b> give back

Proverb: **Mapanga awiri abvumbwitsa.**

**-RA** (-era or -ira) according to the second last vowel of the stem p. 78  
This suffix called the "Applied form" adds a particular note to the meaning of the verb; it generally corresponds to a preposition, such as "to, from, for...":

Munditsekulire chitseko! for me. Anambara katundu usiku from him.  
Timaŵalemba kalata. to them. Mukuphikira yani nsima? for whom  
Ndinadzera ku Lilongwe. through Anathaŵira kutchire. to the bush.  
Tikufunirani chaka chabwino. wish you Ananditumizira ndalama.

If we add the suffix -nji? (What? p. 36) to the applied form, the meaning is "Why", "For what reason?": (Negat. -lekeranji ku...?)

Munalemberanji kalata? Mwadzeranji? — Ndadzera ntchito.  
Mwachitiranji zimenezo? Mwana akuliriranji?  
Mwatiitaniranji? Akudandauliranji?

Mlekeranji kulankhula? Why don't you speak?

Some verbs take a reduplicated suffix:

-seka laugh : -sekera be glad : -sekerera rejoice (because of)  
-kondwa be glad : -kondwera : -kondwerera

It is difficult to give a general rule about the suffix -ra:

There are verbs which take preposition, and not the suffix -ra:

Pereka moni kwa alendoŵa! to Mukufuna kucheza ndi yani? with  
Ndakongola ndalama kwa u'eni from Tsikani mu mtengo! from

Other verbs take neither a preposition nor the suffix -ra:

Ndikubwerekani njinga. to Musandiseke. at  
Anamlanda katundu yense. from Chabwino, ndikuthawani. from

Sometimes the suffix -ra changes completely the meaning of the verb:

-nunkha : -nunkhira. -otha moto : -othera dzuŵa.  
-laŵa : -laŵira take leave; -laŵirira leave early in the morning.  
-cheza : -chezera (moŵa, kubvina...) spend the night doing something.  
-landa : -landira. -samba : -sambira swim

In Verbal adjectives, the suffix -ra shows the particular aim or use of an object or a building. However, there are exceptions.

Ndalama zogulira mabuku. Njerwa zomangira tchalitchi.  
Chingwe chomangira katundu. Khasu lolambulira msewu.  
Nkhwangwa yotemera nkuni. Misomali yokhomera nsungwi.  
Madzi otsukira mbale. but Madzi akumwa: Madzi osamba.  
Nyumba yophikira (Mophikira) kitchen. but Nyumba yogona (Mogona). p. 42

Nyumba yochezera (Mochezera; ...yodyera (Modyera); ...yosambira etc. ...  
but Malo ogona (Pogona); Mphasa yogona (Chogona)

HOW (relative): m'mene, momwe, umo: The verb which follows takes the suffix -ra p. 62.

Mundiuze m'mene mumaphikira ndiwozi! Tell me how you cook this relish.  
Tabwera kudzaona umo mukumangira nkhwake.  
Dzulo anali bwino pang'ono. Sindidziŵa m'mene aliri lero.  
Umu ndimo m'mene timachitira. This is how we do it.

monga m'mene: monga momwe "as, like, in the same way as": the verb which follows takes the suffix -ra. p. 65

Lembani monga m'mene ndalemba ine! Chitani monga momwe mufunira!  
Aliyense achite monga m'mene aganzira iye mwini!  
Aliyense apeske monga momwe angathere! ...according to his means.

more and more: a special construction with -mka or -pita; the verb which follows takes the suffix -ra and is duplicated:

Odziŵa chizungu akumka nachulukirachulukira. more and more numerous.  
Mudzi wao unamka nukulirakulira. grew bigger and bigger. p. 88  
Mbiri yake idzamba nimvekeramvekera ponse ponse. will spread everywhere.  
Ngongole zake zikupitabe m'tsogolo zichulukirachulukira.

Chi—re First meaning: "still" p. 75 Ali chigonere (: Adatagonabe)

Second meaning: "since" Chiyambire since the beginning.

Anthu amasonkhana bwino chiyambire. Chikhalire since it is there.  
Sanapite kuchipatala chibadwire. Chibadwire since (one's) birth.

Bwalo lao linali pamenepa chikhalire has always been here.  
Sindinamve nkhani yotere chikhalire. I have never heard such a story.  
Chifikire chake ku Malaŵi kuno, sanapitense kudziko kwao.

Kuchokera pano mpaka ku Salima tinayenda pagalimoto. From... till: p. 41  
Timagwira ntchito kuyambira lolamba kufikira loweruka.

Mpeni wohekera nyama. Tambala logulira moŵa.  
Tsekera lomangira mpanda. Zitsulo zokonzera njinga.  
Anadzafunsira mbeta pompano. Anakusimbirani zotani?  
Anakubisirani mawu. Kanditolereni nkuni!  
Mundiulire dzina lake! Musavutike za mawa!

Kumudzi kumene munabadwira ndi kwa yani? Ntchito zandichulukira.  
Mnzanu akakulakwirani, muyenera kumkhuŵulukira; musamkwiye!  
Ndadzakubwezerani nkhwangwa ija munandibwereka dzana.  
Mukupseranji mtima? Kodi mawu anga akupitani?  
Mutaona mnzani ali kusauka, musamumire mtima, mumchitire chifundo!

Proverb: Posambira mfulu kapolo asambira pomwepo.



Nthenda	disease	-hemoka	faint
Chimfine	cold in the head	-tsokemola	cough
Litsipa	headache	njenjemera	shiver, tremble
Nthomba	small pox	-temera	vaccinate, make incision
Chikuku	measles	-baya	pierce
Matumbo	bowels	-dzoza	anoint
Nyamakazi	rheumatism	-lumala	be lame
Khate	leprosy	-pola	heal (wound)

-DWA (-edwa or -idwa) according to the second last vowel of the stem p. 78  
This suffix can be considered as a Passive form:

Anihu atatu anaphedwa ...were killed. Munatumidwa ndi yani? By whom...  
muuso mwaitanidwa. Ananyengedwa ndi mazake.

It may also have a reflexive meaning, but it supposes that the action has occurred by accident, not intentionally (p. 76 -dzi-).

Anaphedwa. He killed himself accidentally. Anadzipha (suicide).

Anatamedwa. chala ndi ukhwangwa. He cut his finger with an axe.

The Passive form -dwa has become quite common nowadays, probably through the influence of schools. However it sounds like a corrupted Chicheŵa. It seems preferable to avoid it by using the Active form whenever it is possible.

Kodi anakumenyani? instead of Kodi munamenyedwa?  
Ndinakana kunditama. Ndinakana kutumidwa.  
Mnzanga anandithandiza. Ndinathandizidwa ndi muzanga.

Mwanayu sayenera kumpatsa kanthu. ...sayenera kupatsidwa kanthu.  
Anthu sakonda kuwanyoza pa maso pa anzao. ...kunyozedwa...

There are some abstract nouns made out of the Passive form of a few verbs, with the suffix -dwe and the prefix ka- or ma-. They express the way or manner of doing something.

Kakonzedwe preparation, reparation  
Kaphikidwe way of cooking  
Kabvinidwe way of dancing  
Kaimbidwe melody  
Maonekedwe appearance  
Malimidwe agriculture, cultivation  
Machitidwe manners, behaviour  
Mavalidwe fashion

Khalidwe, Makhaliidwe, Chikhalidwe quality, disposition, character.  
Musayende naye mnyamata ameneyo, ngati alibe makhaliidwe abwino.  
Kwathunso timaimba nyimbo yomweyo, koma kaimbidwe kache ndi kosiya.  
Ndimakonda kwambiri ndiwo zimenezi, koma sindidziwa kaphikidwe kache.

Verbal adjectives are always used in the Active form. Examples where we may find the Passive form -dwa are quite few. Sometimes the stem is reduplicated, to express intensity or perfection.

Zinthu zakuba	Nyama yootcha	Dzira lophika p. 42
Nsaru zochapa	Mbatata zokazinga	Mtambo wakuda
Nkhope yokongola	Mvula yowaza	Nyimbo yotukwana
Zobvala zosachapa	Mnyamata wolumala	Tsitsi losapesa
Madzi otentha	Mphepo yozizira	Zipatso zakupsya
Nyumba yosesasesa	Nsapato zakuthaita worn out	
Ndiwo zophikaphika	Nyama yohekacheka cut into pieces	

Ntchito yoleledwa permitted Cule woletsedwa forbidden.  
Ntchito zolamulidwa Anthu ofedwa mourning.  
Kalata yolembedwa ndi pensulo written in a pencil.  
Panali mnyamata wina wotchedwa Chimwaza Called Chimwaza (tcha call).  
Oitanidwa ndi ambiri koma osankhidwa ndi ochepa.

Anatengedwa ndi mnyamata wa ku Dedza. Katundu yense anabedwa.  
Pakali pano sangafunsidwe mbeta. Mnyamata uja watsutsidwa.  
Dengu langa lija ladiyewa ndi chiswe. Nkhani yake sinakambidwe.  
Mfumu anagwidwa ndi nthenda yoposa. Analumidwa ndi njoka dzana.  
Kufuna kwa Mulungu kuchitidwe! Ana awa sanayesedwe mayeso.

NOUNS Verbal Adjectives are sometimes used as nouns p. 45 with the prefix wo- for persons : Wolumala uja ali bwanji?  
prefix cho- for things (reference to chinthu) :

Ndinamva zotukwana. Zokamba zake zikuchititsa manyazi.  
Ndinaona zodabwitsa. Mutikhululukire zochimwa zathu.  
Anachita zopusa. Ndinapeza zobvuta zambiri.

Many nouns are made out of verbs, but the last vowel -a often changes into -i for persons (prefix m-), or into -o (or -i) for things (sometimes prefix chi- or u-) :

Mlonda watchman	Mbusa shepherd	Mtolankhani reporter
Mphunzitsi teacher	Mlembi secretary	Mi'mi farmer
Mkwati bridegroom	Gonthi deaf person	Mpulumutsi saviour
Dandaulo complaint	Bvuto difficulty	Phunziro lesson
Chilonjezo promise	Chilolezo permission	Chipulumutso salvation
Chikondi Chikwati	Chidani Chibwenzi	Chibale Chinansi
Uphunzitsi Umisiri	Usilikali Ubwenzi	Udani Ulimi Ukwati.

Proverb : Choipa chitsata mwini

Maliseche	nakedness	-nenepa	be fat : -nona (animal)
Mkono	arm	-onda	be lean
Chala	finger, toe	-tsoka	be weak
(m') chiuno	waist	-liimba	be strong, firm, hard
Phewa : Phuza	shoulder	-gwada	kneel
Phazi	foot	-imirira	stand up
Pfupa	bone	-kwaŵa	crawl, creep
Ndedo	stick	-tsimphina	limp

Saweruzika adamanga nyumba pamwala Prov.  
Mbalame ikakhala pa uta silasika.  
Khoswe akakhala pa mkhate sapheka.  
Madzi akatayika saoleka.  
Bvinabvina sabvinika. : Chitachita sachitika.

-gundika be in full swing: Ntchito yagundika. Nyimbo yagundika.  
-kanika be a failure: Fodya wakanika. Mvula yakanika.  
Mwambi umenewu sutanhaulika bwino pa chizungu,  
Nyumba imeneyo simangika; mwini wate adapita kuulendo.  
Munthu uja dzina lake laŵalika.

—ULA suffix sometimes reverses the meaning of the verb; but the examples are few. In many other verbs, the meaning remains substantially the same.

tseka	close	:-tsegula	open	-bvala	put on	:-bvula	take off
mata	glue	:-matula	take off	-funya	fold	:-funyulula	unfold
tola	pick up:	-tula	put down	-bvundikira	cover	-bandukula	uncover
sankha	choose	:-sankhula	choose	-pum?	rest, breathe	-pumula	rest
-yankha	answer:	-yankhula	speak	(:-lankhula)			

SUFFIXES Out of the same stem, we can make many new verbs, by using the various suffixes na-, -tsa-, -ra-, -dwa-, -ka-, -ula.  
Sometimes we find two suffixes joined together :

-ona	see	-bwera	come
-onana	see one another	-bweretsa	cause
-onetsa	show	-bwereza	repeat
-onetsera	show for	-bwerera	come back; bwererana
-oneka	be visible	-bwereka	borrow, lend; bwerekana one another
-onekera	appear	-bweza	give back; -bwezera give back to

The specific value of each suffix helps us to discover the meaning of the derivatives.

However, as a conclusion, it is good to remember that sometimes the suffix changes completely the meaning of the verb, so much so that we do not see any more the connection with the original verb.

-yenda	-dya	-bvuta	-gwira
-yendetsa	-dyetsa	-bvutitsa	-gwirana
-yendetsera	-dyetsera	-bvutana	-gwiriza
-yendera	-dyera	-bvutika	-gwirizana
-yenderana	-dyerera	-bvutikira	-gwiritza

Proverb: Garu wankota sakandira pachabe.

—KA (-eka or -ika) according to the second last vowel of the stem p. 78  
This suffix is another Passive form. It can have two meanings :  
Potential meaning : "can break, will break; is breakable" :  
with the Present tense, more particularly with a negation.

Chingwe chimenecho chiduka.	Kodi phiri likuoneka? is visible
Ndalama zija zipezeka.	Mbale imeneyi sisweka.
Chitsekochi sichitsekeka.	Niwanaya saweruzika.
Ukwati wachikhristu sumasulika.	Mnzanyo satsutsika.
Chitheka it is possible	Ndi chosatheka, it is impossible.

Descriptive meaning : with the Perfect tense. It expresses a situation resulting from an action which has happened recently.

Chingwe chija chaduka is broken	Bukhu lanu laoneka (: lapezeka)
Nsara yake yang'ambika.	Mpando wa mfumu wathyoka. p. 30
Dzira limedzi lasweka.	Nkhope yake yasinthika.
Chitseko chatsekeka (chokha) but	Chitseko chatsekedwa.. by somebody

There are a few verbal adjectives which take the suffix -ka

Uyu ndi mwana wanga wokondeka.	Mfumu wolemekezeka honourable
Uyu munthu wotchuka famous	Uyu ndi munthu wodziwika well known
Ana owerengeka few	Anthu esawerengeka innumerable
Munthu wokhulupirika reliable	Zobvata zong'ambika torn
Zinthu zofunika necessary	Kumudzi kwao ndi kosadziwika.

In a few verbs the suffix -ka has a causative meaning :

-goneka	lay down : Gonekani mwana pamphasa!
-imika	put upright : Imikani mtolo wansungwi!
-dzoka	rub oneself with oil : Mtsikana wadzoka nkhope ndi mafuta.
-bveka or bvaka	clothe somebody : Anabveka mwana malaya ofira.

There are many other verbs ending with -ka which are transitive.

-pweteka, -bwereka, -bereka, -lalika, -pereka; -seteka...

Mtunda	hill, coast	-koka	pull
Mtsinje	river, stream	-kankha	push
Mlatho	bridge : ulalo	-oloka	cross (river, lake)
Mphambano	cross-road	-khweta	turn, bend
Ngelo	cart : garet	-patuka	leave the road, go aside
Bwato	boat	-perekeza	accompany
Sitima	steamer	-lumpha	jump
Pfumbi	dust	-palasa	pedal, paddle
Pafupi	(ndi, pa) near, close	Kufupi (ndi, kwa) M'fupi (mwa)	p. 14. Ntchito yapafupi easy. (wa) mtengo wapafupi cheap Midzi ili m'fupim'fupi close to one another.
Patali	(ndi) far	Kutali (ndi) M'tali (mwa)	p. 14 Ntchito yapatali ndifficult. (wa) mtengo wapatali expensive, dear. Midzi ili m'talim'tali far from one another.
Pakati	(pa) in the middle	M'kati (mwa) in the middle, inside	p. 25 Pakati pabwalo pali chintengo chachikulu. M'kati mwanymba -li ndi pakati be pregnant : -li ndi pathupi: -li ndi mimba.
Panja	(pa) outside	Kunja (kwa) Wakunja	stranger p. 25 Tsukani mphika m'kati ndi panja pomwe! Chakunja the exterior Cham'kati the interior [p. 25, 68]
Pamwamba	(pa) on top, above	Kumwamba (kwa) M'mwamba (mwa)	Dziko la kumwamba heaven. Mau a pamwamba top voice. Mbendera zili m'mwamba. -yang'ana m'mwamba.
Pansi	(pa) at the bottom, below	(Kunsi (kwa) M'nsi (mwa)	p. 25; 68 Dziko la pansi pano earth, world. Mau a pansi low voice. Pansi padengu underneath. Nyumba yao ili kunsi down hill.
Patsogolo	(pa) in front, further on, in the future	Kutsogolo (kwa)	p. 25 M'tsogolo (mwa). Mtsogoleri leader -tsogolera lead. Sitidziwa za m'tsogolo the future.
Pambuyo	(pa) behind, after	Kumbuyo (kwa) M'mbuyo (mwa)	p. 25 -bereka mwana kumbuyo carry on the back Pambuyo pake. A patsogolo aizakhala pambuyo The first will be the last.

Note their particular way of speaking, different from ours:  
Nyumba yao ili pafupi. Onani, apo pali nthochi, ndipo kumbuyo kuno  
(in front here) kuli mtengo waukulu. Tsono nyumba yao ili patsogolo  
apo. (further on, behind)

Pa dzanja lamanja: Pa dzanjadzanja on the right. Ku...  
Pa dzanja lamanzere on the left. Ku manzere to the left.

Kumpoto in, to the north Kumwera in, to the South  
Kum'mawa in, to the East Kumadzulo in, to the West

Faseri	(pa) behind, not visible	Kuseri (kwa) M'seri (mwa)	Khomo lili paseri. Mudzi wao uli kuseri kwaphiri. Ndinakamba naye kuseri privately.
Pamtunda	up hill	Kumtunda -gona pamtunda	sleep on the ground Nyumba yanga ili kumtunda, koma yao ili kunsi down hill. Mimba yake ikucnekera pamtunda is naked Wabvala nsanza zokha.
Patsidya	on the other side of river	Kutsidya...M'tsidya	Amakhala patsidya. Tiyeni ku tsidya! (: tioloke) Ife timakhala m'tsidya lino. on this side.
Patsinde	(pa) at the foot of	Kutsinde (kwa) M'tsinde (mwa)	Tsinde thick end of a pole, tree... Nsonga sharpe end Pa tsinde paphiri Pa tsinde pa mtengo.
Pambali	on the side, aside	Kumbali M'mbali	Musamange nyumba yanu pakati pabwalo koma pambali. Amakhala mbali ya ku Dedza somewhere near... ika ku mbali.
Padera	aside	Dera space, area: Pali dera lalitali lopanda madzi.	Munthu wapadera (:wakunja) stranger, not member of the group. Zinthu zapadera spares. Sali pantchito, ali padera.
Kubwalo	(:kunja) Muyenera kutsuka bwino m'kati ndinso kubwalo.	(:pakhomo) Musalowe nonse muno; ena akhale kubwalo.	(pamtunda) Malaya ang'ambika; mimba yake ikuonekera kubwalo. (kumphala) hut for unmarried youth : Mnyamata wa m'bwalo: wa pamphala : wosakwatira.
Pamphepete	(pa) on the side of	Kumphepete M'mphepete (mwa)	Nyumba yake ili m'mphepete mwa msewu.
Pagombo	la nyanja on the lake shore	Mtunda also means "coast" or "river-bank", the opposite of	madzi : Mtunda ukuonekera uko.
Pamalo	pa in the place of	M'malo mwa instead of M'malo mo- (verb)	Pamaso pa under the eyes of, in the presence of
Pathungo	at the end	Ku... : Kumathero : Kumapeto : Kumalire	border Sitima ya pamadzi; Sitima ya pamtunda (Njanje railway) Njinga yopalasa ; Njinga ya mthuthuthu (Njinga ya moto) Kuchokera pano mpaka ku Dedza pali mtunda wa mamailosi angati? dist- -koka fodya (:suta..) smoke. Ana inu, patukani! Galimoto likubwera. [ance

Proverb : Liwiro la mumchenga nkuyambira limodzi.

Buthu	young girl	-lera	care for, nurse
Namwali	grown up girl	-mana	refuse to give
Bere	breast	-patula	separate
Nchembere	woman with children	-tanganidwa	be busy
Nkhalamba	old person	-khwima	be mature, firm, old
Imvi	grey hair	-sanduka	change into sth. else
imfa	death	-tembenuka	turn round, change
Manda	grave	-gaŵa	divide

**NDI** as a conjunction means "and": *Afate ndi amayi. Usana ndi usiku.*  
 When two verbs follow one another, the second one sometimes takes the Infinitive: *Tinimba ndi kubvina mpaka usiku.*  
*Mulungu amatikonda ndi kutisamala masiku onse.*

Sometimes with the Past tense in the third person, the infix *na-* is dropped in the second verb, and the conjunction *ndi* changes into *n-*:

*Anapifa kumunda nayamba kulima (: ndipo anayamba...)*  
*Anagwa panjinga natlyoka mwendo.*  
*Njoka inadutsa msewu nilowa m'dzenje.*

We have met a similar construction in "more and more" p. 81 :  
*Mabvuto apa ananka nakulirakulira.*

**NDI** as a preposition means "with": *Ana ali kuseŵera ndi mpira.*

Followed by a pronoun, we often find a contraction of vowels p. 48 :

Nane Nawe Naye Nafe Nanu Nawo Ndikufuna kucheza nanu.  
 Naye Nawo Nacho Nayo Nalo Nawo Nako Njinga ndili nayo.  
 Pl. Nawo Nayo Nazo Nazo Nawo Nawo Nato Ndabwera nazo izi.

**NDI** as a verb means "is, are": *Ichi ndi chiyani? (:Ichi n'chiani?) p. 38*  
 It is often joined to the Personal pronoun in a contracted form:

*Ndine Ndiwe Ndiye Ndife Ndinu Ndiwo Mfumu pano ndine p. 38*

It can also be joined to the Demonstratives: "Behold...!" "Here is..."

	Nayu	Nawu	Nachi	Nayi	Nali	Nawu	Naka	Naku
Pl.	Nawa	Nayi	Nazi	Nazi	Nawa	Nawa	Nati	
	Nayo	Nawo	Nacho	Nayo	Nalo	Nawo	Nako	Nako
Pl.	Nawo	Nayo	Nazo	Nazo	Nawo	Nawo	Nato	

*Nayu katundu wanu! Here is your luggage!: Katundu wanu nayu!*  
*Nali funso langa! : Funso langa nali! Naku kudandaula kwanga!*  
*Nawo munda wao! Nayi keyala yanga! Here is my address!*

**NDI** as a verb can also be joined to Adjectives: contraction.

	ngwa-	ngwa-	ncha-	nja-	nla-	ngwa-	nka-	nkwa-
Pl.	nga-	nja-	nza-	nza-	nga-	nga-	nta-	
	ngwo-	ngwo-	ncho-	njo-	nlo-	ngwo-	nko-	nkwo-
Pl.	ngo-	njo-	nzo-	nzo-	ngo-	ngo-	nto-	

*Mwanayu ngwaulesi (: ndi waulesi). Garuyo ngwopusa.*

*Khasuli nla yani? Dziko lino nlokoma.*

*Pa : Pamudzi pano mpa yani? Pakhomo mpotseka.*

*Pamthunzi apa mpabwino. Pakhosi panga mpotupa.*

*Ku : Kumudzi kwanu nkuti? Kuno nkwabwino; uko nkoipa.*

*Kumudzi kwao nkwa yani? Kudziko kwao akosadziwika.*

*Mu : M'nyumba muno mmwabwino. M'nyumba umu mmosasesa.*

*Kunja kokha nkoyera; koma m'kati mmosatsuka.*

**SI** as a verb means "is not, are not" (the opposite of *ndi*) p. 38  
*Nthochi zabwino si izi koma izo. Kodi si zoonza?*

*Si bwino kuti apite yekha kumsika; koma atenge mtsikana mnzake.*  
*Ndinaleka sukulu zoonza; koma si kale kwenikweni.*

With a demonstrative, it can be an exclamation "Here it is!"  
 with reference to an object which has already been mentioned :  
*Siyi mvula ikubwera! Here is the rain coming (as I told you).*  
*Mumafuna mperi; siwu! You were looking for a knife; here it is!*  
*Nyumba yao sili kutali; siyo! There it is! Silzo!*

**Suja...is the equivalent of "Don't you remember?" :**

*Kodi simundizindikira? Suja tinakomana dzulo kumsika?*  
*Kodi mwaiwala dzina lake? Suja ndinakuuzani dzana?*  
*Lero simufuna kuimba chifukwa chiyani? Suja mumakonda kuimba?*

**SI** sometimes expresses intensity, an exclamation "you cannot imagine how much", "extremely": followed by the infinitive and Possessive.

*Anthu amene anasonkhana kumaliro si kuchuluka kwake!*

*Mwanayu akakwera njinga, si kunyada kwake!*

*Si ulesi wake mwanayo! Amangokhala ndipo saweruzika.*

We find a similar construction with the same meaning: *SI* followed by the preposition *pa* and a noun, or the prefix *po-* and a verb :

*Anthu aulesi si pochuluka! Si pa mantha kalulu!*

*Dzuwa likawala, maluwawa si pakukoma! (: si pokoma)*

*Atsikanawa si pakukoma nyimbo zao akabvina pachikwati!*

**LESSON 43**

<b>Chitsononkho</b>	empty cob	<b>KUTI</b>	
<b>Khoko</b>	husk, leaf, skin	-kolola	reap break off
<b>Mtondo</b>	mortar	-tonola	knuckle off grains
<b>Munsi</b>	pestle	-konola	pound maize
<b>Mphale</b>	pounded maize	-gaya	grind
<b>Gaga</b>	bran, husk	-khuthula	pour out
<b>Chimera</b>	malt, sprouted maize	-peta	winnow
<b>Mgaiwa</b>	flour from mill	-bviika	take out water
		-bvuuula	dip, put in water

**KUTI** as a verb has various meanings according to the context :

"say" : Mukuti chiyani? Anthu amati wolakwa ndine.  
 Nditi uyu osati uyo. Akakupatsa kanthu,, uziti: Zikomo!  
 Mfumu uja anayankha nati: Msonkhano udzakhala loweruka.

"think" : Ndinamlembera kalata ndipo ndina!i adzandiyankha.  
 Muli pano? kodi! Ine ndimati munapita kuulendo. thought  
 Inunso muma nwa moŵa! Ine ndinkati simukumwa. thought

"intend" : followed by the Subjunctive; "want", "be about":  
 Ndimati ndifunse. I would like to ask a question.

Ndimati nikuthandizeni Anati achoke dzulo, koma analephera.  
 Akati ayende ankayenda pansu. Gatu anati andilume koma anachita mantha.  
 Anati apite kuulendo pamene anayamba matenda.  
 Ndikati ndimuitane kumsonkhano, mwina sadzabwera.

We find a similar construction in the negative form (infix -sa):  
 it is an invitation to change one's mind :

Musati muchoke! (to somebody who is about to leave or wants to go away)  
 Asati abwerenso kuno! (supposing that he wants to come again)  
 Usati ukwatiwe naye mnyamata ameneyo!

Sometimes the verb **kuti** expresses an attitude or disposition, for instance  
 when it is followed by "ideophones" p. 98:

Ndinangoti chete. I just remained silent.  
 Mwanayu akumva chifuwa; angoti tsoko-tsoko. ... he coughs continually.

Ati! or Eti! (Note intonation) "isn't it" "don't you?" p. 45

Pano mpabwino ati! Nonse muli okondwa eti!

Ati with intonation — "he says" "they say" "it seems":

Akufuna kupita kwao ati. Anamanga nyumba yokoma ati.

Ati... sometimes expresses intensity "extremely"; exclamation cf. Si p. 89

Ati mphepo kuzizira kwake! Dziko lino ati kukoma kwake!

**KUTI** is also found in the form of a Verbal Adjective **Woti, choti, yoti...**  
**Anampatsa dzina loti Fanesi. (: Anamtcha dzina lake Fanesi)**  
**Mawu oti "Basopo" atanthauza chiyani? What means the word Basopo?**

Reduplicated, it means "such-and-such," "so-and-so," "this or that" :

Tinazolowera kulima mwa njira yakuti yakuti...in such-and-such way:  
 Akakupatsani chakutichakuti, musaliwale kumthokoza.  
 Mungapite kwakutikwakuti, mudzamva mbiri yomweyo.  
 Akakuuzani zakutizakuti, musazimve.

Sometimes it introduces a new sentence: we may find 3 constructions:  
 the Subjunctive; the Infinitive n'ku-; the Infix -zi- p. 76

Ndinalibe ganizo loti ndimkwatire mtsikana ameneyo.  
 Sindipeza nthawi yoti ndicheze naye.  
 Palibe chifukwa choti muchite mantha.  
 Nthawi yakwana yoti ndiitule pansu ntchito.

Palibe chifukwa choti nkuchita mantha.  
 M'nyumba muno mulibe malo oti nkuyalamo mphasa ziŵiri.

Ndinaŵapatsa nzeru yoti azikhululukirana.  
 Anatipatsa lamulo loti aliyense azithandiza mnzake.

We should not use the Subjunctive if it is only a statement or a declaration:

Tsiku lamulungu ndi tsiku loti anthu sagwira ntchito.  
 Ndinalandira mthenga woti amayi anga ali kudwala matenda aakulu.  
 Chimene ndinganene ndi ichi chakuti inu mwalakwa. This is what I can say:  
 Chondidabwitsa ine ndi ichi chakuti sanandiŵe kanthu. What surprises me.  
 Chondipira ine ndi ichi chakuti anachoka osalawira. What displeased me...

Osati.. "and not" p. 47: Muzigula malalanje, osati nthochi.

**CHABE** as a noun means "nothing, rubbish, something worthless":

Ndi chabe kumanga nkhekwe ngati mulibe chimanga. It is vain...

As an adjective, it has the same meaning "worthless, of bad quality":

Anandiphikira ndiwo zachabe. (: zopanda pache) p. 38

Anakwatiwa ndi mnyamata wachabechabe. good-for-nothing

An adverb, it means "just, only" p. 39: Ali ndi mwana mmodzi chabe.

Munthu uja sali mphunzitsi konse; ali munthu chabe. (: ...wamba)

Musataye nthawi pachabe! Anakasaka nyama ndipo anabwera chabe.

Mukupita kuti? — Kuyenda chabe. : Kungoyenda)

Proverb : Chakomachakoma pusi anagwa chagada.

Mbiya	beer-pot, jar	-tunga	draw, fetch water
Mtsuko	water-pot	-tapa	take a portion of
Nkhali	cooking-pot	-phula	take off the fire
Chikho	gourd, cup	-funda	be warm
Chipanda	beer-gourd	-wira	boil, bubble
Lichero	flat basket	-bvundikira	cover, put lid on
Nsengwa	small basket	-bvundukula	uncover, take lid off
Mthiko	porridge stick	-bvundula	stir up

**KUTI** is often used as the equivalent of a conjunction: "that" p. 20  
**Ndinamva kuti munapweteke. Anandifunsa kuti: Kodi muli bwino?**  
**Anayankha nati: Ndiliba mawu. (Anayankha ndipo anati: ... p. 88** ...  
 Expressing an order or a wish, it is followed by the Subjunctive :

**Ndinamuuza kuti apite kwao. Salola kuti ndikhale pano.**  
**Ndinamletsa kuti asachoke. ( : Sandileleza kukhala pano)**  
**Ndinamtuma ku sitoro kuti akandigulire fodya.**

Instead of the Subjunctive, we may find the infix **-zi-** p. 76:

**Ndinamuuza kuti azipita kwao. Sindifuna kuti azingokhala.**

Another meaning of **kuti**: "so that" "in order that", with the Subjunctive, or the infix **-zi-**. sometimes **kuti** is dropped.

**Ndinam'bwereka njinga kuti afike msanga.**  
**Mundipatse nyale ija kuti nditsiremo mafuta ( : kuti ndizitsiramo...)**  
**Ndi kusiyirani mpira (kuti) muzisewera nawo :**

The negative form is expressed by the infix **-sa-** or **nga**. p. 74

**Ndinatseka pakhomo kuti ana asalowe munyumba.**  
**Munampatsa ndalama kuti asaulule kanthu. a definite purpose.**  
**Thawani msanga kuti galu angakulumeni. a possibility, occurrence**  
**Musasewera ndi mpeni (kuti) mungapweteke muzanvu..**

**Ndiye kuti...** is a common expression to introduce some explanation; "it is because" "well" "then" :

**Ndikupita kumudzi; ndiye kuti kwathu kwabwera alendo.**  
**Pepani, sindinagule kanthu; ndiye kuti ndinalibe ndalama**  
**Pamudzi pano pagwa maliro; ndiye kuti msonkhano wathu uja wakanika.**  
**Nkhani yomwe ndabwera nayo nayi: ndiye kuti...**  
**Cholemba kalata ndiye kuti The reason why I write... is that...**  
**Chin'hu choyamba chofuna kukudziwitsani ndiko kuti...**  
**Chodzera pano munthune ndiko kuti mfumu anandiitana.**  
**Chimene chikufunika ndithu ndiko kuti tonse tikhale ogwirizana.**

**Si kuti..** is the equivalent of "it does not mean that"; "it is not because.."; "it is not that...":

**Ndinamlembera makalata; koma si kuti ndidzambkwatira ayl.**  
**Uyu sapita kusukulu, sikuti ali kudwala ayi, koma ndi ulesi basi.**  
**Nkuti...** following words such as **nthawi imeneyo, m'menemo, monse...** indicates that "at that moment" some action was in progress:

**Nyumba yanga inapsya dzulo; nthawi imeneyo nkuti ine ndili kudambo.**  
**Tinasonkhanga anthu ambiri; nthawi m'menemo nkuti ili 3 okoloko.**  
**Monse tinkacheza m'nyumba mwao nkuti mvula ili kugwa.**  
**Monse m'mene tinkayenda m'njira muja nkuti nyimbo ili pa kamwa.**

**Poti : Pakuti: Popeza kuti** means "since, because":  
**Tiyeni, tizipita kwathu, poti gule watha.**  
**Pakuti mukumva malungo, simuyenera kugwira ntchito.**  
**Sindinapite ku msonkhano, popeza kuti sanandiitane.**  
**Mungathe kupita kwano, poti mulibe mawu.**

Followed by the Subjunctive, it expresses an intention ( : **kuti**)  
 "as I wanted to...":

**Poti afike msanga kumudzi, anabwereka njinga kwa mnzake.**  
**Poti athawe, anataya katundu panjira.**

**Moti : Mwakuti: Motere kuti: Kotere kuti** expresses a consequence :  
 "so much that", "in such a way that" :  
**Anammenya kopsya, mwakuti satha kuyenda.**  
**Ndinadwala nthawi yaitali moti cha'ka ch'ino sindinalime nawo.**  
**Amakonda kunyenga anzake, kotero kuti muyenera kuchenjera naye.**

**M'malo moti:** with the Subjunctive, means "instead of" :  
**M'malo moti akonze njinga, walononga kwenikweni.**  
**M'malo moti atsire mafuta munyale, anatsiramo madzi.**  
 We find the same meaning with **M'malo mo-** or **Pa malo po-**  
**M'malo mopita ku msika, anapita ku mowa.**  
 With the Subjunctive, **M'malo moti** may also express a purpose :  
 "so that"; "in order that" :

**Tinamphikira chakudya m'malo moti asachoke msanga.**  
**M'malo moti andikhulukire, ndinampatsa nkukhu.**

With the Present tense, it is the equivalent of **Poti "since"** :  
**M'malo moti sindidziwa chisangu, ndingamvane naye bwanji?**  
**M'malo moti mwakana kundithandiza, sindikupatsani kanthu.**

Proverb : **Akuluakulu ndi m'dambo mozimira moto.**

Here is a list of enclitics and various suffixes which are often joined to verbs or other words; for some of them the meaning is evident; but for others it is sometimes difficult to find the equivalent word in English.

- NSO “again” *Nenaninso!* Say it again! *Anso!* Again! p. 19  
 “also” *Inunso chenjerani!* Ali wantali ndinso wonenepa.  
 “any more” *Musadzand! bvtutenso!* Sindidzakuphunzitsaninso.  
*Komanso* but also: *Sanabe ndalama zokha komanso thumba lomwe.*
- BE “still” *Ali kudwalabe.* He is still sick: *Adakadwalabe.* p. 75  
*Ali m'tulobe :* *adakali m'tulo.*  
 “not yet” *Sanafikebe.* He has not yet arrived: *Sangafike.* p. 75  
 -*libe* “have not” : *Alibe bukhu ndi limodzi lomwe.* p. 11, 65  
*Palibe, Mulibe,* “there is no...”, “be absent”. p. 16  
*Anabereka ana asanu ndi awiri, ndipo ali nawobe onse.*  
*Komabe* “however, nevertheless” *Ali bwinopo, komabe sadzachira.*  
*Anandipatsa ndalama zina komabe sizikwanira.*
- DI shows that I agree with what has been said: “indeed, truly, in fact”.  
*Zoonadi!* Quite true! *Ndithudi!* Indeed! *Zedi!*  
*Taanani, myula yabweradi.* *Mfumu uja anali munthu wabwinodi.*  
*Ndinakuzani kuti adzachoka; anachokadi dzulo.*  
*Komadi ( : Koma zoonadi) Komadi muli mwayi ( : muli ndi mwayidi).*
- TU reinforces a statement: “for sure, believe me, really” :  
*Anamanga nyumba yabwinotu. Inetu mowa sindikumwa.*  
*Bwinotu, mungagwetse mwana. Please. be careful... p. 69*  
*Komatu ( : Koma ndithu) Nyumba yake ndi yakale komatu njokongola.*  
 It can also reinforce an order: “Please, don't hesitate, well” :  
*Mveranitu!* Please, listen! *Cherjeranitu!* Please. be prudent!  
*Mayi wako akukuitana, pitatu! Ngati ukufuna kuimba, imbatsu!*  
*Sindingathe kunyamula katunduyu, ndipotu ndingomsiya pompano.*  
 Joined to a verb ending with the suffix *-ra,* (p. 80), the meaning is “do something in advance” or “completely” :  
*Tilandira alendo madzulo. Tiyeni, tikonzeretu malo!*  
*Mukafena kupita mawa ku chaka. muchapiretu lero lomwe!*  
*Ufa watheratu. Chimanga kulibiretu. Pepani, ndaiwaliratu.*
- NO seems to be equivalent of *-tu* in some areas: “well, then” :  
*Komano ( kema tsono) Ndirubwerekani njinga, komano musisamale.*  
*Basino!* Well, that is enough!

—PO means “rather, quite, a little” (reference to *pang'ono*) :  
*Anadwala matenda akulu; koma tsopano ali bwinopo.*  
*Mulaŵepo! Muonjezepo! Zikemo ndilankhulepo.*  
*Ndinamanga nyumbayi kalepa ( : kwapita nthawi yaikulupo)*  
*Anabzala mitengo yechulukirapo. Mwana wanga ali wocheperapo.*

It can also be a Locative (demonstrative) p. 53

*Chotsani katundu pa thebulopa kuti ndiikepo mbalezi!*  
*Mfumu anandipatsa malo awa kuti ndimangepo nyumba yanga.*  
*Chingwe chija chopachikirapo zabvala chaduka.*

—KO joined to a verb, softens an order, or suggests some restriction :  
 “some, to a certain extent” : *Laŵanike! ( : Laŵankoni!) p. 77*  
*Kodi mwadyako? Ndinaphunzirako. Ngakhale chizungu adziwako.*

It can also be a Locative (demonstrative) p. 53

*Ndinapita kumaliro kwa Chinutu; ndipo ndinabwerako dzulo.*  
*Kumudzi kwao sindinapiteko. Kodi inu mukudziwako?*  
*Bwalo lija lopanyerako mpira lili kutsidya.*

—MO is a Locative p. 53. *Nyumba yanga ndi iyi; tiyeni, tilowemo!*  
*Patseni nyale ija kuti nditsiremo mafuta.*  
*Malo osungiramo katundu ndi awa. ( : Mosungira katundu ndi umu)*  
*Nyumba yogonamo alendo ndi iyo. ( : Mogona alendo ndi umo);*  
 Following a noun; *-po, -ko, -mo* are Demonstratives (*apo, uko, umo*);  
 for an object which is near: *-pa, -ku, -mu* (*apa, uku, umu*) p. 66-68

*Khalani pa mpandopa! Pamwambapo pali chiyani?*  
*Ndikupita ku tsidyako. M'nyumbamu mulibe mphasa.*

—NI corresponds to *inu.* It is sometimes postponed p. 77  
*Patsenkoni! ( : Patseniko!) Tigawirenkoni!*  
*Nyale ija ili kuti? Bwera nayeni! (Bwerani nayo!) Anthuni!*

—NJI is the Interrogative pronoun “What?” p. 36 *Mukufunanji?*  
*Mwadzerani p. 80 Palinji?... (Pali chiyani?)*  
*Chifukwa ninji? ( : chifukwa chiyani?)*

*Ndipo* “and” p. 10 *Tengani mwanayo ndipo pitani naye ku chipatala.*  
*“it is no...that” p. 68 Paphiri ndipo (pamene) pali minyala yambiri.*  
*“rather, better” Pansi si pali bwino; koma pamwamba ndipo.*  
 Also *ndiponi; Kulemba sindikhoza; koma kuwerenga ndiponi.*  
*Ndiko* “it is at...that” p. 68 *Kuchipatala ndiko kuli mankhwala abwino.*  
*Ndimo* “it is in...that” p. 68 *Umu ndimo (m'mene) timagona ife.*  
*“this is how” p. 81 Umu ndimo (m'mene) timachitira.*

## LESSON 46

## REDUPLICATION

The repetition of the stem in Adjectives generally corresponds to a superlative and expresses intensity : p. 55, 83

Antku ambirimбири very numerous	Milandu yankhaninkhani numerous
Nyumba yaikulukulu	Chingwe chachitalitali
Kamwana kakang'onong'ono	Zobvala zazifupifupi
Nyumba yosesasesa well swept	Nyimbo zosiyanasiyana various
Nsaru yakuthaitha worn out	Mpeni wakuthwaithwa very sharp
Njinga yakufaifa	Nyama yophikaphika.

With verbs, it expresses frequency or continuity :

Tinabvinabvina mpaka usiku.	Mwanayu amangoliralira.
Anawerengaawerenga kalata ija.	Ndikufunafuna kalata yake.
Amadzapemphapempha ndalama.	Amangolongololalongolola.
Nditakhalakhala pa khomo, mfunu anandiitana.	
Munali kuti? — Timadyaidya mtedza pakhomo apo.	

With Adverbs, it indicates intensity :

Konzani msangamsanga! quickly	Anachita daladala intentionally
Pang'onopang'ono very little	Pang'onopang'ono little by little
Msika uli pafupifupi very near	Ntchito yapatalitali very difficult
Kalekale long ago : Anamwalira kalekale, inu musanabadwe.	
Kalekale soon : Anathamanga kwambiri, kalekale wafika.	
Muziyendetsa njinga bwinobwino gently p. 69	Mwapolepole slowly
Anafotokoza nkhan mwa tsatanetsatane point by point	

With nouns : Akuluakulu elders, important persons

Anabzala mitengo ya mitundumitundu. of various kinds	
Chithunzithunzi picture	Mamvalmva rumours
Chimasomaso seduction	Munthu wa magwiragwira thief
Ndipatseni matambala okhaokha. only pennies p. 60	
Amagona wina pa yekha, wina pa yekha. separately p. 60	
Alliyense akhale ndi bukhu lakelake. his own book p. 34	
Tiuzeni chenicheni! something clear. p. 57	
Pakati penipeni right in the middle. Kwenikweni akufuna chiyani?	
Ponseponse : Konsekonse : Monsemonse everywhere p. 59	
Uku ndi uku here and there. Kwina ndi kwina in the differnt places	
Kambirimbiri often (: kawirikawiri). Tsiku ndi tsiku day by day	
Kale mazira mtengo wake unali khobidikhobidi (: limodzi khobidi)	
Ndinamva zakutizakuti p. 91	Mungathe kuyenda kwakutikwakuti.
Phokoso linanka likulirakulira p. 81	Madzi ananka nacheperachepera.
Reduplication is also found in Ideophones p. 98 Chetechete!	

INTERROGATIONS Here are a few words which are sometimes included in interrogations or exclamations :

<b>Kodi...?</b>	just introduces a question : Kodi mwabwera ndi mawu? It can also be an interjection of surprise Kodi! p. 15
<b>Bwanji...?</b>	"Why?" Bwanji simulankhula mawu? How is it that you do not. "How" Muli bwanji? Mlandu wake unatha bwanji?
<b>Nanga...?</b>	"And what about...? Iwo adya kale; nanga inu? (: kaya inu?) Njinga iyi ndi ya mphunzitsi; nanga iyo? "by the way", "well Muli bwanji nanga (:tsono) Mukupita kuti nanga? Choncho! Titani nanga? "naturally, of course" Inunso mukupita nawo?—Nanga! Ifenso tiyenera kuphunzira chizungu. Nanga! Why not?
<b>Kani...?</b>	shows surprise in presence of something unexpected: "Is that so?" Kani anakhoza mayeso!...Really? he did succeed. Kani amatero! Muli pano kani! Ine ndimati munachoka.
	Monga ntamfunsira mbeta, mungalole kodi? (:...nditamfunsira) that..." the answer is expected to be positive; but in fact it may be negative. Monga mvula ibwera lero? Monga mwakhoza mayeso? Monga mupitadi kuulendo? Sometimes with the infix -ta-, it indicates a supposition: Monga ntamfunsira mbeta, mungalore kodi? (:...nditamfunsira)
<b>Ngati?</b>	expresses a doubt "Do you think that...?; it suggests that the answers will be negative: answer will be negative. Mwanayu amapita kusukulu ngati? Iyayi, amangokhala. Akupita kuti, kuntchito ngati? Iyayi koma ku mowa. Analankhula mawu ngati? Iyayi, anangoti chete.
<b>Eti! (: Atil!)</b>	"Isn't it?" "Don't you?" p. 45; 90
<b>Mwakongwa eti!</b>	Mukabwerenso mawa eti!
<b>Nanji !</b>	"so much the more" "a fortiori": Nyumba iyi njabwino; nanji iyo! Amabvuta mkazi wake masiku onse. Nanji atakhuta mowa!
<b>Malinga</b>	can be considered as a conjunction; it has two meanings : "provided; if" Ungathe kulowa nawo malinga ndiwe mkhristu. Ndigula njinga chaka chino malinga ndikapeza ndalama. Adziwa Chichewa msanga malinga akamachita khama. "according to", "in proportion to" malinga ndi m'mene. Ndidzakulipirani malinga ndi m'mene mwagwirira ntchito. Malinga ndi m'mene amasimbira alendowa, kwao kulibe nvula.
<b>Cholinga</b>	"aim intention" Anabwera ndi cholinga choti atenge mwanayo.

Proverb : Mutu umodzi susenza denga.



In conversation and particularly in narration, we find separate words called "Ideophones". Most of them convey a notion of sound or movement and they make the speech extremely vivid. Here are some examples: it looks like a succession of pictures.

Inetekumudzi mbwe, m'nyumba loŵu, sambeni, pampano khaleni, nkulemba kalata.

Mwana nia mphale bwundu, tsukotsukeni, phu! Muni ti ti ti, mpaka anatsiriza zuzuŵa lili tswi.

Njinga ŵali pa ŵiŵi; adangeza kuti terereku, ndiye phofo pansu khu!

Zi wakomola. nani nyamu ulendo wa kuchipatala; monsemo ali chikomokere.

Note the great variety of forms: some are monosyllabic; others are reduplicated; many of them correspond to a verb and suggest an attitude, a gesture or sound (onomatopoeia).

Mbwe! arrive at: Adayenda msanga; kungoti mbwe wafika.

Phu! be finished: Nsima yatha phu! (Fsi!) nothing left

Tswi! setting down: Dz. ŵa lili tswi! at sunset

Gwa! firm, strong: Ndiri gwa! in excellent condition

Phe! still, motionless: Kkhalani phe! Don't move!

Dzi speechless, silent: Anangoti dz, kusoŵa choyantha.

Chete! quiet, silent: Ine chete, ludabwa. Chetechete santisa nyama.

Se! level, flat: Dziko limgoti se, lopanda mapiri.

Fwa! full: Tili nacho chimanga chambiri; nkhekwe ili fwa.

Mya! smooth, soft: Ubweya weti mya. Marwa a mya.

Zi! nobody in sight: Kujira kuli zi! Alendo aja sabwera.

insipid: Ndiwo za zi. Nkhani ya zi. without interest.

Bi! black, dark: Kwada bi! M'nyumba muno muli bi; tsegulani chitseko!

multitude: Anthu anasonkhana ambiri, kungoti bi kubwalo.

Mbe! white, bright: Kwacha mbe! Maso ake ali mbe, kukondwa.

Mbu! white: Ufa uli mbu! Onse anabwala zoyera, kungoti mbu!

Psyu! red; Magazi ali psyu! Maso ake ali psyu kuyang'ana kunjira.

Firiwiri red; Nsara ya piriwiri. Biriwiri green, blue

(cha) chikasu yellow; (cha) mtambo blue; (cha) msipu green

Dzidzidzi suddenly: Unali ulendo wadzidzidzi. Anafika mwadzidzidzi.

Nda nda nda in a row: Nyumba zili nda nda nda m'nyumbe mwa msewu.

Waliwali shining: Ng'anang'ani glittering: Chzichezi shining.

Balabalalala scatter, disperse: Yayamba mvu'a, anthu angoti balabalalala.

Piringupiringu move to and from; Zwezwe round and round.

—**KHALA** stay, live: Mumakhala kuti? Wakhala pansu zaka zambiri.

sit: Khalani pa mpandopa! Khalani pansu!

be (future) : Mwanayu adzakhala mnyamata wamphamvu. p. 23

subjunctive) : Ambuye akhale nanu!

have future) : Tidzakhala ndi chimanga chambiri chaka chimo.

(subjunctive) : Mwana ali yense akhale ndi bukhu lakelake.

not to go, stay away from : Anakhala kusukulu dzulo.

Munakhalliranj kumsonkhano?

Khalani bwino! (: Tsalani bwino!)

-khalala or -khalira in the negative and followed by the Infinitive indicates that the action takes without delay:

Ndiwozi sizikhala kupsya. ...does not take much time to be cooked.

Amana anga sakhala kupsya mtima. ...gets angry easily.

Mitengoyi sikhallira kukula ndi kubereka zipatso.

**Pokhala** "a place where to stay" : Akusoŵa pokhala. p. 42, 80

"since" (also Poti, Popeza kuti, M'malo moti) p. 93

Simuyenera kutenga njingayo, pokhala mwini wake palibe.

Pokhala kuti ndilibe njinga, sindipita ku msonkhano.

**Akhala** expresses a supposition (conditional) p. 73

Akhala mwalemba kalata, bwenzi nditakuyankhani msanga.

also Kuchikhala kuti mwalemba kalata, bwenzi nditakuyankhani.

**Ngakhale** or -ngakhale "even if, although" p. 74

"either... or" : Onse ali okondwa, ngakhale amuna ngakhale akazi.

**Mphunzitsi sanabwere lero, kapena nkukhala chifukwa cha matenda.**

Chipewachi chikandikhala bwino. fits me

Ndinampeza ali khale. just staying

**INVERSIONS** are quite common in Chicheŵa; here are some more examples.

Munthu wamkulu thupi (: Munthu wa thupi lalikulu) a stout person

Mnyamata wohepa msinkhu (: wa msinkhu wohepa) a short boy

Mtsikana wopunduka miyendo. a lame girl: wolumala

Nyumba yanga khomo lake lopanda chitseko (Khomo lanyumba yanga..)

Mwanayo khalidwe lake si labwino (: Khalidwe la mwanayo.....)

Nkhani imenoyo sindidziŵa kutha kwake, inatha bwanji? Kaya!

Kuyenda amayenda, koma pang'ene pang'ene. He does walk, but slowly.

Kumva ndamva. I have understood what has been said but it does not mean that I agree. We expect something else: Koma

Ndamva. Here no limitation: "agree".

Proverb : Atambwali sametana